

WAMNDEDE



Tiri panonso, mu Dzina la Ambuye Yesu, ndi kudzamva za ntchito zazikulu ndi zamphamvu zimene Inu mwazichita, mmbuyomu. Ndipo tsopano ife taimirira ndi chiyembekezo, zikudzutsa chikhulupiriro chatu ndi kutidzoza ife, kuti tikhulupirire kuti zimene zapemphedwa usikuuno ziperekedwa. Inu mukudziwa china chirichonse cha izo, zonse zimene iwo azipempha. Ndipo ife tikuwapempherera iwo, makamaka, Ambuye, iwo amene ayandikira kufa. Mubweretse mtendere ku moyo wawo ngati mulibemo kale mmenemo. Mubweretse machiritso kwa thupi lawo. Mupereke izi, Ambuye.

² Mudalitse kubwera kwathu pamodzi. Ife—ife tikupemphera, Ambuye, pa msonkhano wa pemphero wa usiku wa Lachitatu uwu, kuti, monga ife tasonkhana, podziwa kuti paliponse pamene awiri kapena ochuluka asonkhana pamodzi, Inu mudzakhala ndi ife. Ndipo ife tikukupemphani Inu, Ambuye, kuti mutipatse ife Mawu Anu usikuuno. Mulankhule ndi ife, Ambuye, ndipo mutenthetse mitima yathu, mwachilendo, kuti ife tikadziwe momwe tingadzikhaliitse tokha akhalidwe chifukwa cha nthawi yopambana imene ili mtsogolo, pamene tikukhulupirira kuti ife tikuyandikira Kudza kwa Ambuye.

³ Ife tikukuthokozani Inu chifukwa anthu tsopano ayamba kupeza chikhulupiriro chokondedwa kwa iwowo, ndipo akudziwa chomwe chikhulupiriro chikutanthauza. Ndi kudziwa, ngakhale kukuthokozani Inu chifukwa cha misonkhano ili mtsogolo, akukhulupirira kuti Inu mudzakhala chinachake. Ambuye, ife tikudikirira ndi chiyembekezo, monga masiku akale, tikukhulupirira kuti nthawi ili pafupi imene Inu muti mudzangokwezera mmwamba mazenera a Kumwamba ndi kutsanulirapo malonjezo amene Mulungu wawalonjeza mu tsiku lotsiriza lino.

⁴ Tsopano ife tikukupemphani Inu, Ambuye, kuti—kuti mukhale nawo onse, kuzungulira mafuko, monga lero ife tamva kuti alipo ambiri kuno, paliponse, amene ali ndi chosowa. Muwapatse iwo zopempha zawo, Ambuye. Ndipo ife tikupemphera kuti tiliwone dzanja lamphamvu la Mulungu likuyenderera pa dziko lonse pakati pa iwo amene akuyembekezera chinthu chachikulu ichi.

⁵ Mutikhulukire ife tchimo lathu. Mutikwapule ife, Ambuye, ndi Mzimu Wanu ndi Mawu Anu, kuti ife mwatokha tikhale akhalidwe, antchito omvera, antchito omvera mu chifuniro cha Mulungu. Mutilole ife tizikumbukira, ndi kuyesera kuganiza mu mitima yathu, chimene Akhristu oyambirira ankachita. Ife tingakumane ndi anthu a mtundu wanji

ngati ife titakumana nawo iwo amene anakumana ndi Inu kwenikweni. Momwe nkhope zawo ziyenera kuti zinkawala ndi chikhulupiriro ndi chisangalalo. Momwe miyoyo yawo iyenera kuti inkakhala Mawu amoyo a Mulungu, basi “akalata olembedwa owerengedwa ndi anthu onse,” pamene iwo ankayenda ndi kukhala pakati pa anthu. Mulungu, perekani izi kamodzinsu.

⁶ Mulole miyoyo yathu ikhale yoperekedwa kwambiri kwa Inu, mwakuti Mzimu Woyera uzidzikhala moyo Wokha kupyolera mwa ife, ndipo mulankhule kudzera mwa ife, Ambuye. Mulole ife tikakumbukire, mmalingaliro mwathu, pamene ife tikuyenda pa msewu ndi kukhudzana nalo dziko, ife sitikuyenera kuti tizikhala monga iwowo. Ndipo ife tiziima pambali ndi kuwapatsa iwo malo, Ambuye, ndipo malo awo owayenera kuno pa dziko lapansi. Ife tizitenga mpando wa kumbuyo, pozindikira kuti ife ndife nthumwi zochokera ku dziko lina. Ife tiri nawo Ufumu umene ukubwera mu mphamvu, Ambuye. Ndipo Mfumu yathu yaikulu ifika posachedwapa ndipo idzatenga maufumu onse amene ali mu ulamuliro Wake. Ndipo Iye azidzalamulira ndi kukhala mfumu; pamodzi ndi Iyeyo kuno pa dziko lapansi, zaka chikwi, ndi kukakhala ndi Iye kwanthawizonse.

⁷ Tiri ndi izi mmalingaliro, Ambuye, tsopano ife tikuyang’ana mtsogolo ku yankho la funso lathu. Ife tikuyang’ana ku chodzinenera chathu. Ngati ife tachita chirichonse, tanena chirichonse, kapena taganizapo chirichonse, chimene chinali chosiyana ndi chifuniro Chanu chachikulu, mulole Magazi a Yesu Khristu atiyeretse ife.

⁸ Mutitsogolere ife, Ambuye, monga mlongo ananena usikuuno, zokhudza iye ndi mwamuna wake akupita ku Chicago. Muwatsogolere iwo, Ambuye Mulungu, mpaka akafike pa malo amene Inu mungathe kukawagwiritsa ntchito, kuti iwowo akakhoze kukhala nyali za kuwala kwa ena amene akupapasa mu mdima, amene sakumudziwa Ambuye wathu Yesu. Tsopano ife tikuwupereka msonkhanowu kwa Inu, ndi kumvetsera Mawu Anu okonza, kuti ife tikakhoze kudziwa momwe tingakonzekere ora lalikulu ili, mu Dzina la Yesu ife tikupempha izi. Amen.

[Malo osajambulidwa pa tepi. M’bale Neville akuchitira ndemanga—Mkonzi.]

Ambuye akudalitseni inu. Zikomo, m’bale.

⁹ Ine sindimayembekezera mpang’ono pomwe izi. Ine, pokhala kuti ndiri kwathu, ine ndimamverera kuti ngati ine sindipitadi kwinkawake, mwadzidzidzi, ine ndikanamverera moyipa kwambiri, ine kungokhala pa khomo ndipo osabwera ku msonkhanu wa pemphero. Ndipo ine ndakhala ngati ndangobwera, mosayembekezeka, kwa inemwini, ngakhale kwa banja langa. Ine ndinangolowa, ndi kungowuyambapo

nthawi yomweyo. Ndipo kotero ine ndinati, “ine ndikupita ku msonkhano wa pemphero.” Ndipo iye sanakhale nayo nkomwe nthawi kuti akonzekere zoti azibwera, kotero iye samadziwa kuti ine ndibwera.

¹⁰ Kotero ndine wokondwa kwambiri kumva umboni wa mlongo apo, m’bale, zokhudza Kuwala kuja uko ku South Carolina kapena North Carolina, kwinakwake. Greenville, ndi kumeneko? [Mlongo akuti, “Ayi. Southern Pines.”—Mkonzi.] Southern Pines. Inde.

¹¹ M’bale Lee Vayle anali komwe kuno lero. Ine ndamubatiza iye, lero, mu utumiki wa ubatizo kuno lero. M’bale Lee Vayle inu mukumudziwa, ndi atumiki uko, M’bale Parker Thomas. Alipo . . .

¹² Ine ndikukumbukira za—za nthawi, mlongo ali ndi mthunzi. Iko kunali kutsimikizira kwakukulu, mlongo, kwa chimene. . . Mzimu Woyera nthawizina umatilola kuti ife tipitirire ndi kukayesa chikhulupiroro chatu, kuti uwone, ndi kukayesa chikhulupiroro cha ena. Pamene iwe ukuyang’anizana molunjika ndi chinachake, ndipo nkumawona chinachake, ndipo nkuchinena icho; ena akayang’ana ndipo osachiwona icho, iwo nkumanena kuti palibepo pamenepo. Mukuona? Koma icho chiri pamenepo.

¹³ Tsopano, panalibe aliyense amene anakhoza kukuwona Kuwala kuja kumene kunapachikika pa Paulo, koma Iko kunali pamenepo. Panalibe mmodzi amene anaiwona nkunda ija ikubwera pansu kuchokera Kumwamba, mu Kuwala kuja, mwamawonekedwe, ndi kudzatera pa Yesu, koma Yohane mwiniwake. Koma Iko kunali pamenepo. Mukuona?

¹⁴ Ndipo kotero, ndiye, mtsogolo pamene ine ndinkawauza anthu za Kuwala uku kuti kunali ngati Lawi la Moto, panalibe aliyense ankafuna kuti akhulupirire zimenezo. Koma tsopano diso la makina la kamera lazindikiritsa Ilo, momwe Iko kunabwerera.

Ndipo mzimu woipa ndi wakuda.

¹⁵ Ziri chimodzimidzi monga miyoyo yathu, ndife mithunzi. Ndipo ife tiri. . . Ngati ife tiri kuwala, pamene ngati miyoyo yathu ikugwirizana ndi Kuwala kwa tsikuli, ife tikuyenda mu Kuwala.

¹⁶ Ziri chimodzimidzi monga inu kuyang’ana panja ndikuti, “Ine ndikuwona dzuwa,” mu nthawi ya masana. Inu—inu mukuwona mthunzi wa dzuwa. Iwo ndi chinyezimiritso cha dzuwa. Si dzuwa limenelo, ilolo, koma izo zikutsimikizira kuti kuli dzuwa. Izo zikutsimikizira kuti kuli dzuwa.

¹⁷ Ndipo tsopano pamene ine ndikukuwonani, monga inu mwakhala panja apo, mukugwiritsa ntchito zokupizira mphepo,

mukulankhula, izo zikutanthauza kuti muli moyo, koma izo ndi mthunzi chabe wa moyo.

¹⁸ Chifukwa, chirichonse chiyenera kukhala ndi mdima mwa icho, kuti chikakhale ndi mthunzi. Mukuona? Chifukwa, mthunzi umayenera kukhala ndi mdima wochuluka kwambiri ndi kuwala kochuluka kwambiri, kuti zikapange mthunzi. Ndipo sizingathe kungokhala mdima basi, ndipo sizingathe kungokhala kuwala basi. Ngati chiri chakuda, chimakhala chakuda kwenikweni. Ngati chiri kuwala, sipamakhala mthunzi, sipamakhala kanthu koti kapange mthunzi. Koma ngati pali kusakanizikana mdima ndi kuwala, izo zimapanga mthunzi.

¹⁹ Chotero ife ndife kwenikweni mithunzi ya kuwala. Tsopano inu mukunyezimiritsa moyo kuchokera kwinakwake. Ngati inu muli, ndipo Mkhristu, ichi pokhala mthunzi, izo zikungotsimikizira kuti ulipo Moyo umene iwe sungathe kufa, chifukwa moyo uwu uli nayo imfa mwa iwo. Mukuona? Koma iwo ndi mthunzi, chifukwa ndinu cholengedwa chamoyo, chomayenda ndi kukhoza kumawona, kuganiza, kusuntha, ndi kulankhula, ndi zokhudzira zisanu za mthupi. Komabe inu mukudziwa, izo, izo ndi zakufa. Ndipo pamakhala mavuto ochuluka kwambiri. Inu mukudziwa, izo zikhoza kukhala basi. . . Ndiko kunyezimiritsa, mukuona, kuti moyo ndi imfa zasakanizikana pamodzi.

²⁰ Chachithupi chiyenera kuti chife. Koma ngati inu mukunyezimiritsa, mwa moyo wanu wachivundi, Kuwala kwa Kumwamba, ndiye kuti inu mukunyezimiritsa Moyo Wamuyaya, Mulungu. Ndiye pamene inu mudzafa, inu simudzachitiranso mwina koma kudzapita ku Kuwala kumeneko, chifukwa Ndicho chimene inu mmachinyezimiritsa.

²¹ Ngati inu muli a dziko la mdima, inu mumanyezimiritsa chimenecho, ndipo inu mukhoza kuchita, simungapite kwina kulikonse koma ku mdima. Mukuona? Kotero ife tiri mu chinyezimiritsa. Chotero, ife tikuziwona zimenezo. Ndipo ndithudi monga Mzimu Woyera umanyezimiritsa Kuwala ndi Moyo, chomwechonso imfa imawonetsa mdima.

²² Ndipo apa ziripo zonse ziwiri. Mawa-...Pakutha pa sabata ino, mwinamwake pofika Lamlungu, ife tikhala ndi chithunzi chaching'onocho chitakulitsidwa kukhala chachikulu, kuti chidzakhoze kuikidwa pa bolodi la zolengeza.

²³ Pamene, chithunzi *chanu* chapachikidwa kunja uko pa bolodi la zolengeza. Ine sindikudziwa ngati inu munachiwona icho, kapena ayi. Ndiyeno. . .

Ndipo pafupi sabata yapitayo, mu—mu Jamaica, kumene ine ndimachita umishonare. Ife timatumiza matepi pa dziko lonse. Ndipo *Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri* zakafika mpaka. . . njira yonse mpaka mkati mwa Jamaica, kukalowa mpaka mkati. Ndipo ndi kwa chimidzi kumeneko, kuseri kwa Blue Mountain.

Ndipo anthu akumeneko, nthawizina, iwo amakhala ndi—ndi tepi rekoda imene tinawapezera iwo, imene iwe umayenera kuti—kuti, monga ya Victrola yachikale, umayipukusa iyo, ndiyeno umaisiya—umaisiya iyo iziyimba monga choncho. Ndiye, maminiti pang’ono aliwonse, winawake amaneyera kuti ayipukuse iyo.

²⁴ Gulu ili linali ndi—ndi batire laling’ono, batire la mavoti sikisi, kapena chinachake chimzake, kumasewerera tepi rekoda imeneyo. Ndipo iwo—iwo onse anali atakhala palimodzi, pafupifupi mmene ziriri usikuuno, kumamvetsera *Zisindikizo* zimenezo, ine ndikukhulupirira izo zinali. Ndipo pamene ine ndimalankhula, iwo anazindikira, kubwera mu chipindacho, panabwera Lawi la Moto lomwe lija, linadzasuntha pamene panali tepi rekoda ndipo linadzakhala pamwamba pa iyo. Ndipo iwo anapita ndipo anakatenga kamera ndipo anajambula chithunzi cha Ilo. Ndipo linali Limodzi lomwe lija, ndi Ilo pamenepo, litapachikika pamenepo. Tsopano ife tikuchikulitsa icho, kuti tikachiike icho pa—bolodi la zolengeza panja uko, kuti inu mukakhoze kuchiwona icho.

²⁵ Ife tiri oyamikira kwambiri chifukwa cha chisomo cha Mulungu chimene chabweretsedwa kwa...ife kufika mu Kukhalapo Kwake mu tsiku lino. Tsopano ife tikuyamikira chifukwa cha zinthu zambiri.

²⁶ Tsopano ine ndikuganiza ine ndiyang’ana apa ndipo ndiwona ngati ine ndingathe kupeza, zolemba zina kapena zina, chinachake chimzake chimene ine ndinayankhulapo. Kapena, kupeza mtundu wina wa—a . . .Ine ndalemba phunziro lina apa, mulimonse, kumbuyo kuno mu bukhu. Ngati ine ndingapeze china, mwina wake Ambuye andipatsa ine chinachake choti ndilankhulepo pa chinachake, pamene ife tikupemphera.

Tsopano ife tiri kuyembekezera Lamlungu.

²⁷ Ine ndakhala ndikulankhula mu Mauthenga. Ndipo, Lamlungu, ndinakusungani pano nthawi yaitali, pa, “Iwe ukulirira chiyani kwa ine? Lankhula kwa anthuwo ndipo uzipita chitsogolo.”

²⁸ Tsopano, Lamlungu tidzakhala ndi msonkhano wamachiritso pamene odwala adzakhala akupemphereredwa. Tsopano, iwe ukafika kwa odwala, ndipo apo pamayenera kukhala chifukwa china chimene odwala, pamene ife tiwapempherera iwo, ngati iwo sakuchiritsidwa. Ndipo ine ndikufuna kuti, ngati Ambuye alola, kudzangokhala ndi ulaliki wawufupi Lamlungu mmawa, aponso. Koteri, ine ndidzakhala ndi msonkhano wa machiritso, ndi kudzawapempherera anthu onse. Ndipo Billy Paul kapena ena a iwo adzakhala ali pano Lamlungu mmawa, pafupi eyiti koloko, pamene tchalitchi chimatsegulidwa, kuti adzawapatse anthu makadi pamene iwo azidzalowa pakhomo, kapena nthawi iliyonse akamalowa.

²⁹ Ndipo tsopano, ndiye, ine ndikufuna kuti ndidzayesere, ine ndikukhulupirira Ambuye pang'ono pokha andipatsa ine kuyang'ana kwa mkati pang'ono pa zifukwa zimene anthu ena samachiritsidwa. Ndipo i—ine ndikukhulupirira kuti ndi kusowa kwa kumvetsetsa. Ndipo i—ine ndikukhulupirira, mwinamwake, ife tidzalankhula pa zimenezo, Lamlungu mmawa, Ambuye akalola.

³⁰ Tsopano, msonkhano wa pemphero wa Lachitatu usiku umangokhala msonkhano wawufupi pamene ife timasonkhana pamodzi ndi kupemphera, monga ife timachitira, ndi kuyanana limodzi.

³¹ Nthawizina, i—ine ndikukhulupirira chimodzi cha zinthu zopambana chimene ine ndimachepeza mu tsiku lino, ndi kusowa kwa kuwona mtima pa zimene ife tikuzikhulupirira. Mukuona? Mukuona? Ngati Mulungu, mu masiku a John Wesley, akanachita mu tsiku limenelo zimene Iye wazichita lero, kodi izo zikanachita chiani; mu masiku a Marteni Lutera, kapena ena onsewo? Pakuti zimene ife tamuwona Iye akuchita, zatsimikiziridwa ndi Mpingo, ndi Mzimu; ndi sayansi, ndi kusuntha kulikonse, m—mphamvu yake iyenera kuzindikiridwa. Ndipo Mawu a Mulungu pano akumazilengeza Izo ndi kumazinena Izo zisanafike Izo podzachitika. Ndiyeno akumayendayenda pamenepo, ndi kumalosera, ndi kumasonyeza chinthu kumene chimene Iye anachinena. Izo nkumachitika mwangwirowo, ndendende zimene Iye ananena. Ndipo komabe ife timakhala olobodoka, ngati kuti iye tikudabwa. “Chabwino, ndikudabwa ngati zimenezo zikutanthauza ine? Ndikudabwa ngati izo zikutanthauza basi—mpingo, wonse. Kapena—kapena, ndikudabwa ngati ine ndaikidwamo kwenikweni mu Chimenecho?” Ine ndikuganiza, Lamlungu mmawa, ine ndidzayesera kuti ndidzalankhule pa zina za mfundo zimenezo zimene zikhoza kutiwalitsira ife pang'ono.

³² Tsopano, usikuuno, ine ndinapeza chinachake, kuti tingotembenukira kwa icho pano, ine ndisanabwere kuno. Ine ndinaganiza, “Bwanji ngati M'bale Neville, ngati ine nditakafika kumeneko iye akakapezeka akunena kuti, ‘Imirirani ndipo mulankhule,’ ndipo ndi kungokhala pansu?” Mukuona? Ine ndinaganiza, “Ine kulibwino ndilembe Malemba angapo.” Chifukwa, ine ndikudziwa, iye, iyeyo ndi m'bale wabwino kwambiri, ndipo i—ife timamuyamikira iye.

³³ Ife tisanawapempherere Mawu, ine ndikufuna kuti ndimuzindikire m—m'bale. Ine ndikulephera ngakhale kuti ndimutichule dzina lake pa nthawi ino, awiri a iwo. Iwo ali pano, amzanga a ine. A...Iwowo ndi atumiki ndi avangeli, mu ntchitoyi, amapita kunjako. Iwo anamvetsera Mauthenga awa pa tepi. Ndipo iwowo ndi ochokera ku mipingo ya zipembedzo zosiyana, anyamata awiri achichepere. Ndipo

mnyamatayo ali motero, mmodzi wa iwo ndi wokondweretsedwa kwambiri, mpaka iye anawuluka kubwera kuno, Tucson, posakhalitsapa, potsekera msonkhano. Ine ndikukhulupirira ine ndinali mu Kadzutsa wa Amuna Azamalonda. Ndipo mnyamata wamng'onoyo, mnyamata wamng'ono wabwino, anabwera kumeneko. Ndipo iye ali. . .

³⁴ Iwo ndi ochokera ku Kansas. Ndipo iwo abwera njira yonse kuno kuti ine ndidzawakwatitse iwo. Ine ndikuyamikira zimenezo. Kuganiza za anthu amene amakhulupirira mmapemphero ako, mokwanira, amakhulupirira kuti Mulungu akhoza kukumva ndi kukuyankha; anyamatawo akuyamba mmoyo, monga chonchi. Ndipo pamene iwo anadzafika kuno kuti ine ndiwakwatitse iwo, dzulo, anadzapeza zimene lamulo la boma la Indiana limafuna, ndipo mpaka kuti magazi awo ayezedwe, kuti adikirire kuno mu bomali, masiku atatu, asanafike poti akwatitsidwe. Koteru, iwo sakwatitsidwa mpaka Lachisanu mmawa.

³⁵ Ndipo ine ndimupempha m'bale wathu apo pamapeto, ngati iye angaimirire ndi kuti iya ife yemwe iye ali, ndi dona wake wamng'ono wokondedwa pamenepo, ndi m'bale winayo.

³⁶ [M'bale akuti, "Zikomo inu, M'bale Branham. Ndi chamwayi kudzakhalana pano. Ndipo ine. . . M'bale Roger ndi ine timakhala ku Kansas, timayenda mtchire, ngati avangeli, kumanena kuti, 'Yesu amapulumsa, amachiza, mwa chikhulupiriro mwa Yesu. . . ? . . .' Ine nthawizonse ndimanyamula. . . ? . . . Uyu ndi amene woti ndimukwatire wanga, Patricia Brown. Ife tidzakwatirana, Lachisanu. Mvangeli mzanga ndi wogwira naye ntchito, M'bale Ronnie. . . ? . . . kumapetoko. Ndi Bambo Peetree chimodzimodzi. . . ? . . ."—Mkonzi.]

³⁷ Zikomo, kwambiri. Ife ndithudi tikuwafunira akazembe achichepere awa, ku ntchito ya Ambuye Yesu, madalitso a Mulungu, kuti awafulumizitse iwo panjirayi. Ndipo pamene ine ndikulingalira, kuyembekezera Kudza kwa Ambuye, ndipo nkumawawona anyamata ndi atsikana ali ndi cholinga mu mtima, kuti azimutumikira Khristu, zimenezo zimandikondoweza ine, mukuona, kuwawona iwo akukula monga chonchi. Ambuye akudalitseni inu, mochuluka, m'bale wanga, mlongo.

³⁸ Tsopano tiyeni ife titembenezire ku Bukhu laling'ono limene ine sindinayambe ndalilankhulapo, mu moyo wanga. Ndipo ilo kwenikweni. . . Chaputala chimodzi chokha, Bukhu la Filimoni. Ndipo ndilo. . .

³⁹ Ine ndine wa chi Irish pang'ono, ndipo ine—ndipo ine ndiri ndi waya kuzungulira mano anga a mmusi, kuti azigwirizira angapo mmbuyomo pamalo awo. Nthawizina ine sindimawatchula maina amenewa molondola, pamene ine ndikudziwa chimene iwo ali. Ndipo nthawizina ine

ndimalephera kuti ndiwatchule iwowo molondola, chifukwa cha kusaphunzira. Chotero, “Filimoni,” winawake ananena kumbuyo uko, chimene ine ndikuganiza ndiko kwenikweni kutchula kolondola kwa iwo.

⁴⁰ Tsopano, ndime yoyamba, ine ndikufuna kuti nditenge mawu amodzi okha kapena awiri kuchokera pamenepo.

Paulo, wamndende wa Yesu Khristu, . . .

⁴¹ Ndipo ndi chimene ine ndikufuna kuti ndigwiritse ntchito usikuuno, ngati mutu, Ambuye akalola, ndi: *Wamndende*.

⁴² Tsopano, inu mukhoza kuvutika kuti mumulingalire Paulo kumadzitchula yekha wamndende. Munthu wobadwa-mfulu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, komabe iye akudzitchula yekha “wamndende.”

⁴³ Ndipo tsopano ife tikupeza kuti, pamene iye akulankhula ndi aku Korinto, “Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu.” Nthawi ina, “Paulo, wantchito wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu,” pamene iye akulankhula kwa Timoteo, osiyanasiyana awo. Tsopano pamene iye akulembera apa kwa Filimoni, iye anati, “Paulo, wamndende wa Yesu Khristu.” “Paulo, mtumwi,” ine ndikufuna kuti ndidzalalikire usiku wina pa zimenezo. “Paulo, wa—wantchito,” ndidzalalikira pa zimenezo. Ndipo kenako, “Paulo, wamndende.”

⁴⁴ Koma, usikuuno, pokhala kuti zikhoza kutenga maora kuti tilingalilepo mofatsa amodzi a maphunzirowo, ine ndikufuna kuti nditenge, usikuuno, “Paulo, wamndende,” ndi kutenga phunziro lakuti: *Wamndende*.

Tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

⁴⁵ Ambuye Yesu, munthu aliyense, amene ali wokhoza mwathupi, akhoza kusolola masamba a Baibulo ili, koma Mzimu Woyera wokha ukhoza kuwatanthauzira Iwo mu kuwala kumene izo zinalingaliridwa. Iye tikumupempha Iye kuti abwere tsopano ndi kudzatithandiza ife kuti timvetse chimene izi zinali, zalembedwerako, mneneri wamkulu, wamphamvu uyu, Paulo, ndipo eti nkumadzitchula yekha “wamndende.” Mulole Mzimu Woyera uwululire izi kwa ife pamene ife tikudikirira pa Iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

⁴⁶ Tsopano ine ndikukhoza kulingalira, Paulo, pamene iye ankalembe kalata iyi kwa Filimoni, momwe iye anali atakhala mu ndende, cha kumeneko mu ndende ya mzinda uwu, wa—wa—wamndende. Ndipo iye amakhoza kudziwa bwino, ndi kumalo komwe iye anali chimene mawuwo amatanthauza. Iye anazunguliridwa ndi—ndi—ndi zitsulo. I—iye amakhoza kokha kumasuka wina akumulola iye kuti amasuke. Ndipo iye ankadziwa chimene icho chinali kukhala wamndende. Ndiyeno, apanso, ine ndikukhulupirira kuti—mtumwi ankatanthauza pang’ono chabe. . . osati kwenikweni kulankhula za chimene

iyе anali panthawiyi, kuti anali wamndende wa—wathupi lake lomwe atakhala apa mu—ndende iyi. Koma ine ndikukhulupirira iyе anali akunena za—umunthu wake, mzimu wa—wa—wake, chifuniro chake, kuti anali wamndende wa Yesu Khristu.

⁴⁷ Tsopano, ife tonse tinabadwa, ochita mwakufuna kwathu, kuti tizipanga chigamulo chirichonse chimene ife tikuchifuna. Mulungu mwachilungamo amachita zimenezo. Chifukwa, Iye amayenera kuti amuike munthu aliyense pa malo ofanana, kapena Iye anamuika munthu wolakwika pa. . . Iye anamuika munthu woyamba pa malo olakwika, kuti Iye anamuika iyе poti azichita mwakufuna kwake. Mukuona? Ife tiri chimodzimidzi, usikuuno, monga Adamu ndi Eva. Palibe kusiyana ayi. Chabwino ndi choipa chaikidwa pamaso pa aliyense wa ife. Moyo ndi imfa, ife tikhoza kupanga kusankha kwathu; ziri ndi inu, kuti muchite zimenezo. Mukuona?

⁴⁸ Umo ndi momwe Adamu ndi Eva anachitira, ndipo, taonani, ndipo—ndipo iwo anapanga kusankha kolakwika. Ndipo tsopano, pochita zimenezo, zinaika mtundu wonse, mtundu wa munthu, pansi pa imfa, chilango cha imfa.

⁴⁹ Ndiyeno Mulungu anadzabwera pansi mmawonekedwe a munthu ndipo anadzatenga imfa imeneyo, ndipo analipira chilango cha imfa, kuti. . . Anthu Ake amene ankakhumba kuti—kuti akhale afulu akakhale afulu.

⁵⁰ Tsopano, ngati Iye atatitenga ife, osati mwanjira yomweyo imene Iye anachitira Adamu ndi Eva, kungitikokeramo ife kudutsa chinachake, kuti, “Ine ndikupulumutsani inu kaya inu mukufuna kupulumutsidwa kapena ayi,” ndiye kuti Iye anamuika Adamu ndi Eva pa—pa maziko olakwika, inu mukuwona. Koma mmodzi aliyense wa ife ayenera kuti asankhe, lero, pakati pa imfa ndi moyo. Ife tikhoza kuchita zimenezo.

⁵¹ Monga ine ndafotokoza kumene, ngati kuwala kwanu kungatsimikizire, moyo wanu udzatsimikizira ndendende mbali imene inu muliko. Ine sindikusamala kuti inu mukuti muli mbali iti. Chimene inu mumachita, tsiku lirilonse, zimatsimikizira chimene inu muli. Inu munamvapo zozona zakale, “Moyo wanu ukuphokosera kwambiri, ine ndikulephera kuti ndimve umboni wanu.” Mukuona? Zochita zanu—zikuphokosera kwambiri.

⁵² Ine nthawizonse ndimakhulupirira mu kufuula ndi kulumpha. Koma ine nthawizonse ndimanena kuti, “Musamalumphe mmwamba kuposa moyo wanu, chifukwa dziko liziyang’ana zimenezo.” Mukuona? Inu muzingolumpha mokwera monga momwe inu mungakhalire moyo, momwemo, chifukwa winawake akukuyang’anani inu. Ndipo tsopano pamene. . .

⁵³ Anthu samabwera ku tchalitchi. Iwo—iwo, ambiri a iwo, samatero basi. Ndipo ena a iwo, amene samabwera, ndi anthu owona mtima. Iwo awona chivundi chochuluka mu

tchalitchi, mpaka iwo samafuna kuti akhale ndi chirichonse chochita ndi zimenezo. Ndipo nthawi zambiri, ife tikulankhula pa lingaliro losapysatira pa zimenezo, inu simungawaimbe nkomwe mulandu iwowo, mukuona, chifukwa cha—cha momwe anthu amachitira. Iwo amadzitcha okha Akhristu. Iwowo ndi chopunthwitsa chachikulu chimene dziko liri nacho, ndi mwamuna ndi mkazi amene amadzinenera kuti ndi Mkhristu, ndipo nkumakhala chinachake chosiyana ndi kudzinenera kwawoko. Kulondola ndendende.

⁵⁴ Tsopano, pakuti kukhumudwa kudzakhala kukubwera pa Chiweruzo. Tsopano, wochimwa, wotcheza mowa, wanjuga, wachigololo, i—iye sakakhumudwa kudzamva chigamulo chake chikuwerengedwa, “Kuti apite ku moto wosatha.” Iye sakakhumudwitsidwa. Koma munthu uyo amene akuyesera kuti azidzibisa yekha kumbuyo kwa mtundu wina wa kudzinenera kwa tchalitchi, ameneyo ndi mnyamata amene ati akakhumudwe pa Tsiku la Chiweruzo. Mukuona? Yemwe amadzinenera kuti ndi Mkhristu, ndipo nkumakhala mwanjira ina yake. Zikanakhala bwino ngati iye akanati asapange kudzinenera kwa mtundu uliwonse, akanati asatero, kusiyana ndi kuyamba ndi kumakhala chinachake chosiyana. Chifukwa, iyeyo ndi chopunthwitsa chachikulu chimene ife tiri nacho, ndi wodzinenera uyo amene amanena kuti i—iye—iye ndi Mkhristu, ndipo nkumakhala chinachake chosiyana.

⁵⁵ Nthawizonse, musamawuweruze moyo wanu ndi mphamvu zomwe inu muli muli nazo zochitira zozizwitsa. Ndipo ife tisamadziweruze tokha ndi kuchuluka kwa chidziwitso chimene inu muli nacho cha Mawu. Koma nthawizonse muzidziweruza nokha, muziyang’ana mmbuyo ndi kukafufuza mtundu wa chipatso chimene moyo umene inu mukukhala pakali pano ukubereka. Mukuona?

⁵⁶ Monga ine ndinalalikira kanthawi kapitako, ku msonkhano wa amuna azamalonda ku Phoenix, Arizona, za chinyezimiritsa cha Yesu, kunyezimiritsa Moyo wa Chikhristu. Ine ndinanena kuti ine ndinabadwira kuno mu Kentucky, komwe kuli kwachimidzi kwambiri, makamaka mmbuyo pamene ine ndinali mwana. Ndipo mnyamata wina wamng’ono uyu analibe nkomwe—n—n—nyumba monga ife tiri nayo kuno, kumene ife tinali ndi akazi okongola ambiri omwe amayenera kuti aziziyang’anira mmakalilole, akamadutsa mnyumba monse, kuti tsitsi lawo lizikhala pamalo ake, ndi zina zotero. Koma iye anali naye kalilole mmodzi wamng’ono, chidutswa chaching’ono chabe chitakhomeredwa pa mtengo panja, kumene kunali chithabwa chosambirapo, kumene amayi ake ndi bambo ankasambirako, ndipo iwo ankapeserapo tsitsi lawo, ndi zina zotero, pa kachidutswa kakang’ono ka kalilole kakale aka katakhomeredwa pa mtengo.

57 Kunena moona, uwo ndi mtundu wa khomo umene ife tiri nawo. Aliyense akafuna kuti awone kalilole, ife ana, ife tinkatenga bokosi ndi kukakwererapo pa chithabwa chosambiracho, ndi kumadziyang'anira pa chidutswa ichi cha—cha kalilole chimene ine ndinatola, ndekha, ku dzala. Kumeneko sikunali ku Kentucky. Uko kunali kuno mu Indiana, uko ku Utica Pike.

58 Tsopano, mwana wamng'ono uyu anali asanaziwone yekha kwenikweni monga choncho. Chotero, iye anabwera ku tawuni, kudzawachezera agogo ake aakazi. Ndipo pa . . . Zinali pamene amayendera chipinda, agogo aakaziwo anali ndi nyumba imene inali ndi kalilole wamphumphu pa chitseko. Ndipo kotero, mnyamata wamng'onoyo, akuthamanga kudutsa—chipindacho, anamuwona mnyamata wina wamng'ono patsogolo pa iye. Ndipo mnyamata wamng'onoyo amathamanga, nayenso. Kotero iye anaganiza kuti ayime maminiti pang'ono kuti awone chimene mwana wamng'ono uyo ati achite. Ndipo pamene iye anaima, mwana wamng'onoyo anaima. Pamene iye anatembenuza mutu wake, mnyamata wamng'onoyo anatembenuza mutu wake. Iye anakanda mutu wake, mnyamata wamng'onoyo anakanda wake. Potsiriza, anayandikira, kuti afufuze. Ndipo iye anapotoloka. Ndipo amayi ake anali akumuyang'ana iye, ndipo agogo ake aakazi, amadabwitsidwa. Anati, “Bwanji, amayi, ameneyo ndi ine.”

59 Kotero ine ndinati, zimenezo, “Ife, nafenso, tikunyezimiritsa chinachake.” Mukuona? Moyo wathu ukunyezimiritsidwa.

60 Ndipo tsopano, ngati ife tikanakhala mmasiku a Nowa, kodi ife tikanatenga mbali ya ndani? Kodi ife tikanatenga mbali ya ndani mu tsiku lija lopambana limene Nowa anakhalamo? Kodi ife tikanatenga mbali iti mu masiku a Mose? Mbali iti mu masiku a Eliya, mneneri, pamene dziko lonse linamezedwa mu—chikhamu chachikulu cha—cha umakono, monga Yezebeli wamakono, ndipo anali atawatengera antchito onse a Ambuye kukalowa mu njira ya chidziko? Ndipo mpingo ndi ansembe onse anali kumugwadira iye. Kodi inu mukanatenga mbali ya kutchuka, kapena kodi inu mukanaima ndi Eliya?

61 Tsopano, ndipo mu masiku a Ambuye Yesu, pamene ife tikanaganiza za Munthu wosatchuka uyu, wosaphunzitsidwa ndi dziko, wopanda masukulu amene akanawapeza konse kuti Iye anapitako, ndipo analibe—chomuchitikira cha ku seminare. Ndi—ndiyeno nkumakula ndi dzina lakuti “wobadwa pathengo.” Ndipo kenako nkutulukira, akulalikira Uthenga umene unali wosiyana ndi chirichonse chimene iwo anali ataphunzitsidwa. Kwambiri . . . Ndi kumawadzudzula atumiki ndi mabungwe awo, ndi zina zotero.

62 Ndipo mabungwe anali a—a—atanena kuti, “Ngati munthu aliyense ayerekeza kupita kuti akamumvetsere wotchedwa

mneneri uyu, achotsedwa mu sunagogi,” limene linali—tchimo lakufa nalo. Iwo amayenera kuti azengedwe mlandu. Njira yokhayo yomwe iwo akanamapembedza inali pansu pa magazi a mwanawankhosa. Iwo ankayenera kuti abwere ku nsembe iyi. Ndipo—ndiyeno iwo anali akunja, ndipo chinali chinthu chachikulu bwanji chimenecho.

⁶³ Ndipo Munthu uyu sanazisamale zinthu ngati zimenezo. Ndipo komabe Iye anakhala mwanangwiro ndi Lemba, koma osati monga momwe iwo amawadziwira Iwo. Kodi inu mukadatenga mbali iti? Mukuona? Tsopano, kodi... Moyo wanu umene mukukhala tsopano, ukunyezimiritsa tsopano chimene inu mukachita nthawi imeneyo, chifukwa inu mwadzazidwa ndi mzimu womwewo. Mukuona? Ngati inu mukutenga mbali imeneyo tsopano, ndi iwo, inu mukadachita izo nthawi imeneyo. Chifukwa, mzimu womwewo umene uli mwa inu tsopano unali pa anthu nthawi imeneyo. Mukuona?

⁶⁴ Mdierekezi samawuchotsapo mzimu wake; iye amangosamuka pa munthu mmodzi nkupita pa wina.

⁶⁵ Mulungu samachotsapo Mzimu Wake, nayenso; Iwo umapita kuchokera pa wina kupita pa winayo. Mukuona?

⁶⁶ Chotero, Mzimu womwewo umene unali pa Eliya unadzabwera pa Elisha, womwe womwewo pa Yohane Mbatizi, ndi ena otero.

⁶⁷ Mzimu Woyera, unali pa Khristu, unadzabwera pa ophunzira, mpaka mmusi, ndipo ukadalibe pa anthu. Inu mukuona? Mulungu samachotsa Mzimu Wake.

Chotero apo ife tasiyidwa, kuti tipange kusankha.

⁶⁸ Ndipo i—ine sindikutha kuwona apa pamene Paulo ankandaula chirichonse, ndi kumanena kuti akudzimvera chisoni kuti iye ndi wamndende. Koma iye anali akulankhula yekha... Ine ndikukhulupirira kuti Paulo, pamene iye ankalembe kalata iyi ndi cholemba chimenecho, kuti izo unali Mzimu Woyera ukumupangitsa iye kuti alembe zimenezo. Kuti, mwinamwake, ngakhale mpaka usiku uno, ife tikukhoza kusolola nkhani ya phunziro lathu, kuti tikasonyeze chifukwa chimene Paulo anachitira izi. Chifukwa, ndi za Mwamalemba, ndipo Malemba ndi Amuyaya. Ine ndikukhulupirira, kuti, atakhala mu mndende yamdima yakale iyi, kuti Paulo ankawalemba amzake apa, kuti, m'bale wake, kuti iye anali “wamndende wa Yesu Khristu.” Kotero, iye amakhoza kuzifotokoza izo powona zomwe zinali zitamuzungulira iye. Tsopano, iye anali mu ndende, koma izo sizinali zimene iye ankazikamba, wa—wa ntchito wa Khristu uyu, mtumiki limodzi naye. Iye amanena kuti iye anali wamndende ku Mawu a Yesu Khristu, chifukwa Khristu ndi Mawu.

⁶⁹ Ndipo Paulo anali sikolala wamkulu mu tsiku lake. Iye anali nako kukhumba kwakukulu. Iye anali—iye anali m—

m—munthu amene anali ataphunzitsidwa, ndi anthu, munthu dzina lake Gamalieli, amene anali mphunzitsi wamkulu wa tsiku lake, amodzi a masukulu aakulu amene iye akanapitako. Mwachitsanzo, monga ife timanena. Wheaton, kapena Bob Jones, kapena sukulu ina yaikulu yachikhazikitso. Iye anali ataphunzitsidwa ngati—ngati—ngati mtumiki wa Mawu. Ndipo iye anali wophunzitsidwa bwino, ndiponso wanzeru, ndi mnyamata waluntha wokhala ndi kukhumba kwakukulu kuti mwinamwake tsiku lina adzakhale wansembe kapena wansembe wamkulu kwa anthu ake.

⁷⁰ Iye anali nako kukhumba. Ndiyeno kudzazipeza, kuti, kukhumba kwakukulu uku kumene iye anali ataphunzitsidwira, ndipo iye anali atakhala moyo wake wonse, kuyambira mwinamwake usinkhu wa pafupifupi zaka eyiti kapena teni, kufika mpaka pafupifupi sate kapena sate-faifi, pamene iye anatsiriza ku koleji ndi kupatsidwa zomuyenereza; ndipo anali nawo madipuloma ake ndi chirichonse, ndipo nkumaima bwino ndi a—alaliki onse, ngakhale kwa wansembe wamkulu ku Yerusalemu. Iye anatumidwa ndi iyeyo, kuchita kutumidwa iyeyo, zolembedwa, ndipo anamudalira Saulo wamkulu uyu, “Kuti apite uko ku Damasiko ndi kukawapeza onse awo amene ankapembedza Mulungu mosiyana ndi zimene iye amanena, ndipo kuti akawamange iwo ndi kukawaika iwo mu ndende. Ngati kutakhala kofunikira, iye anatumidwa kuti akawaphe iwo, ngati iye akanafuna kuti atero.” Iye anali. . . Iye anali ndi kukhumba kwakukulu.

⁷¹ Ndipo tsopano, zonse zomwe iye anaphunzirira nazo, Mulungu anali atazichotsamo izo mwa iye. Mukuona? Ndipo zomwe zinali zolinga zake, ndi chimene bambo ake anali atawonongera ndalama, ndi zokhumba za abambo ake ndi amake, zonsezo zinali zitachotsedwa kwa iye chifukwa chakuti—chakuti Mulungu anali ndi chinachakenso. Choncho, iye anali wamndende kwa zolinga zake zimene iye anali nazo mu moyo, ndipo iye anali atakhala wamndende kwa Yesu Khristu, Yemwe anali Mawu.

⁷² Njira ija yaku Damasiko inamusintha Paulo. Akupita kumeneko, pafupi leveni koloko, mwinamwake, masana, pamene iye anakanthidwira pansu. Ndipo iye anamva Liwu, likuti, “Saulo, chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?” Ndipo iye anayang’ana mmwamba. Ndipo atayang’ana mmwamba, pokhala Myuda, ndipo anadziwa kuti Lawi la Moto ilo linali Ambuye limene linkawatsogolera ana a Israeli, chifukwa iye anadziwa kuti ndi chimene Ilo linali.

⁷³ Kumbukirani, wa Chihebri uyu sakanati achitchule chirichonse “Ambuye,” chilembo chachikulu A-m-b-u-y-e, Elohim, kupatula iye atakhutitsidwa kuti ndi chimene Icho chinali, chifukwa iye anali sikolala wophunzitsidwa. Ndipo pamene iye anayang’ana mmwamba, ndipo iye nkuwona

Kuwala, Uku, Lawi la Moto limene linali litawatsogolera anthu ake kudutsa mchipululu. Ndipo iye anati, “Ambuye,” Elohim, chilembo chachikulu A-m-b-u- . . . “Ambuye, Ndinu Ndani?”

⁷⁴ Ndipo chinali chodabwitsa bwanji kwa wazaumulungu uyu, atanena kuti, “Ndine Yesu,” Yemwe yemweyo amene iye amatsutsana naye. Kunali—kunali kutembenuka kotani! O! O! Icho chiyenera kuti chinali chinachake chowopsya kwa munthu uyu, kuti zokhumba zake zonse zimene iye anali nazo, kudzazipeza kuti, zonse mwakamodzi, iye anali akuzizunza. Zokhumba zake zinali zitamupititsa iye ku—kutali kuchoka ku chinthu chenichenicho chimene iye ankanthauza kuti achite. Ndipo kunali—kudzidzimutsidwa kotani kumene kunali, kwa mtumwi uyu, pamene Iye anati, “Ndine Yesu,” Yemweyo amene iye anali kumuzunza. “Chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

⁷⁵ Chobwereza china chaching’ono chimene ife tikhoza kugwetsera apa. Inu mukuwona, pamene iwo awuseka Mpingo, iwo sikuti kwenikweni amakhala akuwuseka Mpingo, iwo akumuseka Yesu. “Chifukwa chiani iwe ukundizunza Ine?” Zikanatheka bwanji kuti Paulo pa nthawi imeneyo, ali ndi luntha lake lonse, kukhulupirira kuti Ichi chinali . . . kuti Gulu ili limene iye anali kulizunza linali Mulungu kumene yemwe iye ankanadinera kuti akumutumikira? Ine ndikuganiza ndizo, popanda kupita mwatsatanetsatane, ine ndikuganiza ndife tonse ophunzitsidwa mokwanira kudziwa chimene ine ndikutanthauza apa. Chinthu chomwecho chikuchitika lero.

⁷⁶ Paulo, mwakusadziwa, komabe anali wanzeru ndi wophunzira, wophunzira kwambiri kuposa Agalileya osaphunzira awo amene iye anali kuwazunza, amene anali mwa kudzichepetsa kwawo atamulandira kale Munthu uyu ngati Ambuye. Koma, Paulo, mwa kuphunzitsa kwake kwakukulu ndi luntha lake, samatha kuvomereza Zimenezo. Ndipo kunali kutembenuka kotani kwa iye, pa njira iyi. Ndipo iye anali atakanthidwa ndi khungu, kuti iye asachitense utumiki wake, koma iye anatsogoleredwa kuti apite ku khwalala lotchedwa Lolunjika, ndi ku nyumba ya wina.

⁷⁷ Ndiyeno panabwera mneneri kumusi uko, dzina lake Hananiya, yemwe anawona mmasomphenya, iye akubwera kumeneko, anamuwona pamene iye anali, anapita kumene iye anali, ndipo anakalowa mkati. Ndipo anati, “M’bale Saulo, Ambuye anawonekera kwa inu pa njira uko; wandituma ine, kuti ine ndikhoze kuyika manja anga pa inu, ndipo inu mulandire kupenya kwanu ndipo mudzazidwe ndi Mzimu Woyera.”

⁷⁸ Mukuwona kumene iye anali. I—icho chiyenera kuti chinali chinthu bwanji kwa Paulo! Mukuona? Zonse zomwe iye anali ataphunzitsidwa kuti azichite zinali zitatembenezidwa. Kotero tsopano, ndi—ndi maphunziro onse amene iye anali nawo, izo—izo zinangokhala zopanda pake kwa iye.

⁷⁹ Tsopano, iye ankadziwa kuti iye anali ndi chomuchitikira. Kotero apa pali phunziro lina labwino kwa ife, kuti, chokuchitikira chokha ndi chosakwanira. Icho chimayenera kukhala chokuchitikira molingana ndi Mawu a Ambuye. Kotero, iye powona ichi, ndi podziwa kuti Icho chinali Chinachake chachikulu, ndiye, winawake uyo anali atachilandira Ichi asanatero iyeyo, iye anatenga zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi kumeneko—chipululu mu Arabia; akulitenga—Baibulo, monga momwe Ilo linaliri panthawiyu, Chipangano Chakale, ndi kumapita kumeneko, kuti—kuti akafanizitse chomuchitikira ichi chimene iye anali nacho, ndi kukawona ngati Icho chinali Mwamalemba.

⁸⁰ Tsopano bwanji ngati iye akanati, “Chabwino, ine ndikuganiza izo zinali zongodutsana nazo pang’ono chabe,” ndipo nkumapitirira? “Ine nditsatira luntha langa”?

⁸¹ Tsopano, iye amayenera kuti akhale mu ndende kwa chinachake, ndende. Kotero atatha kufanizitsa izo, ndi kuziwona, nzosadabwitsa iye anakhoza kulemba Bukhu la Ahebri, mwa choimira. Mukuona? Zaka zitatu ndi theka ali kumeneko, akuwayala Mawu, ndi kumapeza kuti Mulungu kumene amene anamuitana iye anali akumutengera iye mmbuyo, ndi kumusinthana luntha lake lonse, kumusinthana zonse zomwe iye anazilingalirapo, zonse zomwe iye anaphunzitsidwa kuti adzakhale. Zokhumba zake zonse, anangozipukuta izo kuzichotsa pa iye, ndipo iye anadzakhala wa mndende. Chikondi cha Mulungu chinali chitakhala chopambana kwambiri, ndipo—vumbulutso loterolo, mwakuti iye sakanakhoza kuti achokeko kwa Ilo.

⁸² Ndicho chokuchitikira choona cha wokhulupirira weniweni aliyense amene amakomana ndi Mulungu. I—iwe umafika pokhudzana ndi Chinachake chimene chimakhala chopambana kwambiri, mwakuti iwe. . . .mwakuti—mwakuti iwe umadzakhala wa—wa mndende, kwa china chirichonsecho. Mukuona? I—iwe umachoka kwa chirichonse, kuti ukaziyiwe wekha mu ndende ya Izi.

⁸³ Zinafotokozedwapo nthawi ina pamene Yesu anati, “Ufumu wa Kumwamba uli ngati chinachake monga munthu wogula ngale. Ndiye pamene iye apeza Ngale yodula iyo, iye amagulitsa zonse zimene iye ali nazo, kuti akatenge Imeneyo.”

⁸⁴ Ndipo ndi momwe apa. I—inu muli ndi kulingalira kwa luntha, inu muli ndi—ndi—ndi—chokuchitikirani cha ku sukulu ya zaumulungu; koma pamene ifika nthawi imene iwe—iwe—iwe uchipeza kwenikweni Chinthu chenichenicho, i—iwe umangodziguulitsa chirichonse, ndipo iwe umadzitsekera wekha mu Ichi.

⁸⁵ Paulo ankadziwa chimene icho chinali. I—iye anadzipeza kuti iye anali atamangidwa goli kwa Chinachake. Monga

ife timamuika ka—ka—kavalolo pa goli, ndi kuti—ndikuti azikoka chinachake. Ndipo Paulo ankadziwa, pambuyo pa chomuchitikira ichi, ndi zaka zitatu ndi theka akufanizitsa—chomuchitikira chimene iye anali nacho, ndi Baibulo, iye anazindikira kuti Mulungu anali atamusankha iye ndipo anali atamumanga iye pa goli mwa Mzimu Woyera, chomuchitikira chimene iye anali nacho, kuti azikalalikirira Uthenga pakati pa Amitundu. Mzimu, Iwoweni, unamumanga iye goli.

⁸⁶ Ndipo, lero, monga antchito a Khristu, ife timakhala omangidwa goli, tamangidwa. Ife sitingathe kupita. Ndife omangidwa limodzi ndi Iwo, omangidwa goli kwa Mawu. Ziribe kanthu kuti wina aliyense akunena chiyani, iwe umakhala womangidwa goli kwa Iwo. Pali chinachake cha Iwo, mwakuti iwe sungathe basi kuchoka kwa Iwo. Iwe wamangidwa goli ndi Iwo, mwa Mzimu Woyera, wakumangilira iwe goli kwa Mawu. Ziribe kanthu kuti wina akuti chiyani, Iwo ndi Mawu. Amene nthawizonse amakhala atamangidwa goli ndi Iwo, kuyikidwa mu goli limodzi ndi Iwo. Ku Mawu, mwa Mzimu, iye anali atamangidwa goli.

⁸⁷ Iye anali ataphunzira—kuseri kwa chipululu cha Arabia uko. Pamene, zinthu zake zakale zonse, ndi zomuchitikira, ndi zokhumba, zimenezo, iye anali atavulidwa zinthu zimenezo.

⁸⁸ Tsopano, apo ndi pamene ife tikupeza, lero, kuti ife tiyenera kuti tivulidwe, poyamba. Ndipo anthu samafuna kuti avulidwe. M'bale wa chi Methodisti akufuna kuti agwire pang'ono za kuphunzitsa kwake kwa chi Methodisti. U-hu. M'bale wa chi Baptisti akufuna kuti agwire pang'ono chiphunzitsa chake cha chi Baptisti. Mukuona? Koma iwe unayenera kuti uvulidwe mwamtheradi chichonse, ndipo nkungobadwa kachiwiri, mwatsopano. Ndi kumapitirira kuyambira pamenepo, kuwulola Mzimu Woyera kuti uzikutsogolerani. Inu simunganene kuti, “Chabwino, tsopano, a—adadi anga anati, pamene iwo analowa, analowa mu tchalitchi, iwo anagwirana chanza ndi abusa. Iwo, ndi membala wabwino wokhulupirika.” Izo zikhoza kukhala kuti zinali zabwino kwa liwiro lawo, koma ife tiri mu liwiro lina. Mukuona? Tsopano ife tiyenera kuti tibwerere ku nthawi za Baibulo za tsiku lino.

⁸⁹ Ansembe anamangidwa goli, nawonso. Koma, inu mukuona, iwo anali atalowerera mu ka m'badwo kena, ndipo iwo—iwo analephera kuti avule goli lawo lakale ndi kuvala goli latsopano.

⁹⁰ Ndipo chinthu chomwecho ife tikuchipeza lero. Ife tinabwera kudutsa m'badwo wa chipembedzo, monga ife tinatsimikizira kudutsa mibadwo ya mpingo, Baibulo, ndi zina zotero, koma ife tabwera tsopano ku m'badwo wa ufulu, umene Mzimu Woyera Kumene umabwera pansu ndi kudzazitsimikizira Wokha, ndi kudzazipanga Wokha kudziwika, kudzapanga

lonjezo lirilonse limene Iye analonjeza, kufika pochitika. O, mai! Ndi nthawi yopambana bwanji!

⁹¹ Ndipo iye ankadziwa zimenezo, chinthu china, iye ankadziwa kuti iye sakanatha kumapita ku malo. Pokhala, kuti anali atamangidwa goli kwa Ichi, kuti iye sakanatha. Izo iye ankachita, koma i—iye ankafuna kuti azipita. Iye ankadziwa kuti chokhumba chake chinkamukokera iye pakati pa abale kumene iye amaitanidwa kuti abwere, ndipo komabe iye amakhala wokakamizidwa mu Mzimu kuti akachite chinachakenso. Iye sanali iye mwini.

⁹² Mwinamwake winawake amakhoza kunena kuti, “M’bale Saulo, M’bale Paulo, ife tikufuna kuti inu mubwere kuno, chifukwa ife tiri ndi mpingo wawukulu kwambiri. Ife tiri ndi gulu lalikulu. Zopereka zanu zidzakhala zazikulu, ndi zina zotero.”

⁹³ Koma pokhala kuti anali wokakamizika mu Mzimu, iye amaganiza, “Ine ndiri ndi m’bale uko. Ine ndikufuna kuti ndipiteko ndi kukamupulumutsa m’bale uyu, ndikamutengere iye kwa Ambuye.” Koma, apabe, Mzimu umamukakamiza iye kuti apite kwina kwake. Iye anali wa mndende. Kulondola.

⁹⁴ O Mulungu, tipangeni ife a mndende monga choncho, tichoke ku zokhumba zozikonda zathu, ndi kuchoka ku kaweruzidwe kathu komwe ndi njira yathu yabwino ya kaganizidwe, kuti tikakhale wa mndende wa Yesu Khristu. Ine ndikuganiza kuti ilo linali neno lalikulu, lakuti, “Ndine wa mndende kwa Yesu Khristu.”

⁹⁵ Ndipo kumbukirani, Iye ndi Mawu. Mukuona? Ziribe kanthu kuti wina akuganiza chiani, iwo ndi Mawu. Mukuona? Ngati ndiwe wa mndende kwa Mawu, palibe chipembedzo chimene chingakuchotse iwe kwa Iwo. Iwo—iwo ndi Mawu. Ndinu basi. . . Ndiwe wa mndende kwa Iwo, basi zokhazo. Iwe uyenera kumachita momwe Iwo akuchitira.

⁹⁶ Tsopano, iye samatha kupita ku malo ena amene iye ankafuna, chifukwa (chiyani?) Mzimu unkamuletsa iye. Kumbukirani, nthawi zambiri, zimene Paulo ankayesera kuti apite ku malo ena, kumaganiza, “Uko ndi kumene ine ndingakakhoze kukakhala ndi msonkhano waukulu,” koma Mzimu umakhoza kumuletsa iye. Tsopano, kodi zimenezo zikufotokoza momveka ndi kutsimikizira kuti Paulo anali wa mndende? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Wa mndende kwa Yesu Khristu, womangidwira goli ku Mawu Ake, mwa Mzimu! O! Ine ndikuzikonda zimenezo. U-huh.

⁹⁷ Iye anali atamangidwa. Iye anali atamangidwa ndi unyolo, ndi zingwe za chikondi, kuti azikachita chifuniro cha Mulungu, ndipo chokhacho basi. Iye anali wa mndende. Iye anali mu unyolo wa chikondi. Iye anali mu goli ndi Khristu. Iye sakanakhala pa goli ndi chinachake. Iye anali pa goli ndi

Iye. Ndipo kumene kutsogolera kumapita, ndiko kumene iye amayenera kuti azipita. Zinalibe kanthu kuti kumeneko kunali msipu wobiriwira, kuno ku mbali *iyi* kapena mbali *iyoy*, iye ankayenera kuti azipita njira imene Mtsogoleri ndi goli zimapita.

⁹⁸ O, usikuuno, ngati ife, monga Branham Tabernacle, tikanangokhala amndende; kwa umunthu wathu wozikonda, kwa zokhumba zathu zomwe, mwakuti ife nkukhoza kudzipereka kwathunthu tokha ndi kukhala pa goli kwa Iye, ziribe kanthu kuti dziko lonse likuganiza chiani, zimene dziko lonse likuchita. Ife tamangidwa ndi zingwe za chikondi. Ife ndi amndende. “Mapazi anga ali pa goli kwambiri kwa Khristu, iwo sangavine. Maso anga amangidwa goli kwambiri kwa Khristu, kufikira kuti ine, pamene ine ndiwawona odzivula amakono awa pa msewu, Iwo amatembenuza mutu wanga. M—mtima wanga uli pa goli kwambiri mu chikondi ndi Iye, kufikira kuti ndikulephera kukhala pa chikondi ndi dziko lino, panonso. Chifuniro changa chiri pa goli kwambiri kwa Iye, mpaka kuti ine sindikudziwa nkomwe tsopano zomwe ziri zokhumba zanga. Basi, ‘Kulikonse kumene Inu munditsogolera, ine ndidzatsatira, Ambuye.’ Ine ndidzakhala wa mndende.” Mukuona?

⁹⁹ Paulo anali molondoladi wa mndende. Iye sanali kupanga neno lolakwika lililonse. Iye anaphunzitsidwa ndi Mzimu Woyera, apanso, kuti azidikirira pa Mawu. Tsopano, iye anali ataphunzitsidwa njira yina, koma—koma Mulungu anali atamuphunzitsira iye njira ina tsopano. Iye anaphunzitsidwa ndi Mzimu Woyera kuti azidikirira pa Ambuye, zinalibe kanthu kuti zokhumba zake zinali chiani.

¹⁰⁰ Tsopano ine ndikufuna kuti, mothandizidwa ndi Mzimu Woyera, ndikusonyezeni inu chinachake. Mukuona? Tsopano tiyeni tingotenga mwachitsanzo.

¹⁰¹ Tsiku lina, Paulo ndi Sila, akubwera chotsika mu msewu mu mzinda winawake kumene iwo anali kuchititsa chitsitsimutso. Ndipo mtsikana, wamng’ono wodzazidwa ndi ziwanda anakhala akumutsatira iye, akumulirira iye. Ndipo sindikukaikira kuti Paulo ankadziwa kuti iye anali nawo udindo, ngati mtumwi, kuti awudzudzule mzimu woipa uwo kuti uchoke mwa mkaziyo. Koma kodi inu munazindikira? Iye anadikirira, tsiku ndi tsiku, mpaka, mwadzidzidzi, Mzimu Woyera unalankhula ndi iye, unati, “Ora lake ndi lino.”

¹⁰² Ndiye iye anati, “Iwe mzimu, tuluka mwa iye.” Mukuona? Iye ankadziwa kuyembekezera pa Ambuye.

¹⁰³ Ndipo apo ndi pamene anthu ambiri lero amabweretsa chitonzo pa Mawu. Iwo amapita ndi chikhumbo. Ndi zitsitsimutso zingati zimene zangosiyidwa matalala chifukwa cha chinthu ngati chimenecho, chifukwa mvangeli samayembekezera kuti awone chimene Ambuye ati anene!

Ena a iwo amati, “Bwerani kuno,” ndipo iwo—iwo amapita nthawi yomweyo chifukwa gulu lanena kuti, “Pitani.” Ndipo Mzimu Woyera ukhoza kunena chinachake chosiyana. Komabe, chokhumba cha munthuyo ndi chakuti adzakhale woyang’anira deralo, kapena—kapena chinachake chimzake, kapena eledala wina, kapena bishopu wina, kapena chinachake chomukoka iye, “Iwe uyenera kuti uzipita.” Ndipo, komabe, iye akudziwa bwino. Mzimu Woyera ukuti, “Pita *uko*.” Mukuona? Iye wamangidwa goli kwa bungwe lake. Iyeyo ndi wa mndende kwa bungwelo.

104 Koma ngati iye wamangidwa goli kwa Khristu, iye azitsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Iye...?..Mukuona? Iye, iye wamangidwa goli, wa mndende. Sizimapanga kusiyana kulikonse ndi chimene chirichonse chinena; ndi—ndi—ndi—mkuwa wophokosera ndi nguli yolira. Iye amamva kokha Liwu la Mulungu, ndipo iye amalankhula kokha pamene Ilo litulukira. Iye samanena kanthu kalikonse.

105 Wina akati, “O, o, M’bale Jones!” M’bale Roberts, kapena wina, amuna aakulu awa mu dziko lathu lero, monga Tommy Hicks, ka—ka—kapena Oral Roberts, ka—kapena M’bale Tommy Osborn, ena a avangeli opambana awa. Ngati winawake atanena kuti, “Atati, mubwere kuno, Tommy. Inu ndi munthu wopambana wa Mulungu.” (Kapena Oral.) “Ndipo i—ine ndiri ndi—amalume amene agona kuno, amene—amene angomangidwa. Ndipo iwo—iwo akudwala. Ine ndikufuna kuti inu mubwere kuno. Ine ndikukhulupirira kuti inu muli nazo mphamvu zoti muwachize iwo.” Mukuona?

Ndipo mwinamwake Mzimu Woyera unganene kwa iye, “Osati tspano.”

106 Koma, apobe, chifukwa cha ubwenzi ndi munthu ameneyo, iye amakhala wokakamizidwa kuti apite ndi iye. Ngati iye satero, iye amadzakhala mdani kwa munthu ameneyo. Munthu ameneyo amati, “Chabwino, iye anapita kwa *wakuti-ndi-wakuti*, anakamuchiza mwana uyo kapena mnyamata uyo. Ine ndikudziwa iye anatero. Ndipo ine ndakhala ndi bwenzi wake, kwa zaka, mukuona, ndipo iye sanabwere ku malo anga.”

107 Koma ngati iye wakakamizidwa ndi Mzimu Woyera kuti asapiteko, iyeyo kulibwino asapiteko, ngati iye wamangidwa goli kwa Mulungu. Bwenzi wakeyo, iye amamukonda. Koma iye kulibwino azitsogozedwa ndi Mzimu Woyera kuti apite kumeneko, chifukwa izo sizingamuchitire ubwino uliwonse, mulimonse. Ine ndimakomana nazo zimenezo nthawi zambiri.

108 Koma Paulo anangoyembekezera kuti Mzimu umuuze iye choti achite. “Uzidikirira pa Mzimu,” anatero. Iye anaima usiku wina, akulalikira. Ndipo iye anachokako kumeneko. Iye anamuwona bambo wolumala. Ndipo zonse mwakamodzi, Mzimu unalankhula naye iye, ndipo iye anati, “ine ndawona.” Motani? Momwemo momwe iye anawonera kuti akukachita

ngozi, pa chisumbu. Mukuona? “Ine ndawona kuti inu muli nacho chikhulupiro kuti muchiritsidwe. Imirirani pa mapazi anu. Yesu Khristu wakuchiritsani inu.” Mukuona? Ndi zimenezotu. I—iye anali. . .Iye anali pa goli. Iye mwina anali atachititsa chitsitsimutso cha sabata kumeneko ndipo kunalibe chimene chinachitika, komabe iye anayembekezera pa Mzimu Woyera kuti ulankhule. Mukuona? Iye anali pa goli kwa machitidwe amenewo.

¹⁰⁹ Tsopano inu mukuti, “M’bale Branham, inu mukutsutsana ndi zimene inu munanena Lamlungu, zakuti inu mwakhala mukudikirira nthawi yonseyi.”

¹¹⁰ Ndipo, koma, inu mukukumbukira, izo unali Mzimu Woyera umene unalankhula ndi ine uko pa msewu, ndipo unati, “Ine ndikukutumiza iwe ubwerere pakati pa odwala ndi osautsika.” Mukuona? Ndi kumvera kwa Mzimu Woyera. Ine sindinapite kufikira Iye atadzandiuza ine kuti ndichite zimenezo. Ine ndinali ndikudikirira PAKUTI ATERO AMBUYE, mpaka ine nditalandira PAKUTI ATERO AMBUYE. Tsopano, izo ndizosiyana. Mukuona? Tsopano, Izo, Izo zikupanga kusiyana. Inde.

¹¹¹ Iye anayembekezera pa Mawu a Ambuye. Iye anali wopsyinjika mu Mzimu, kuti azingochita kuitana kwa Mulungu basi, ndiye iye anadzakhala wa mndende wa Yesu Khristu. Abwenzi, ngati ife titangokhala basi amndende!

¹¹² Ine ndikudziwa kwatentha. Koma i—ine ndikufuna kuti nditchule anthu angapo, ngati inu mungatero. Ine ndiri nawo pafupifupi sikisi kapena eyiti ndawalemba apa. Koma i—ine ndikufuna kuti ndimutchule munthu wina kapena awiri.

¹¹³ Tiyeni ife titenge khalidwe la Mose. Iye anabadwa ali wowombola. Ndipo i—i—iye ankadziwa zimenezo, kuti iye anabadwa ali wowombola.

¹¹⁴ Koma ine ndisananene za Mose, ine ndikufuna kuti ndinene neno ili, lakuti, Mulungu nthawizonse amayenera kuti amutenge munthu aliyense, amene ati adzamutumikire Iye moon, kuti akhale wa mndende Wake. Munthuyo amayenera kuti akapereke chokhumba chirichonse chimene iye ali nacho, chirichonse chimene iye ali, chiri—chirichonse, moyo wake, solo, thupi, chifuniro, zokhumba, ndi china chirichonse, ndipo nkukakhala wa mndende wamphumphu, kwa Khristu, Amene ali Mawu, kuti azikamutumikira Mulungu.

¹¹⁵ Iwe ukhoza kumayenda mosiyana, mu kaweruzidwe kako kabwino. Mwinamwake, mu bungwe linalake, iwe ukhoza kumaganiza kuti iwo akhoza kukakukweza iwe mmwamba ndi kukakupatsa iwe chinachake chachikulu, chimene iwe ukhoza kumawonetsera. Koma kodi iwe umadzipeza wekha uli chiyani? Iwe umadzipeza wekha utagonjetsedwa, pakapita kanthawi,

kufikira Mulungu atamupeza munthu amene akulolera kuti akhale wa mndende kwa Iye.

¹¹⁶ Mulungu akufunafuna a mndende. Iye nthawizonse wakhala akuchita zimenezo. Inu mukhoza kuzifufufza izo kudutsa Lemba. Munthuyo amayenera kuti akakhale wa mndende kwa Khristu, motsutsana ndi chirichonse. Choncho, inu simungakhoze kulumikizana ndi chirichonse koma Khristu; ngakhale abambo anu, amayi anu, m'bale wanu, mlongo wanu, amuna anu, akazi anu, aliyenseyo. Inu mumangolumikizana ndi Khristu yekha, ndipo Iyeyo basi, ndiye Mulungu akhoza kukugwiritsani inu ntchito. Kufikira pamene, inu simungathe.

¹¹⁷ Ndikamapita uko, nthawizina ndimalankhula mwankhanza kwa anthu. Mukuona? I—ine ndikuyesera kuti inu mumasuke. Inu muyenera kukhala ndi malo oyambira, monga nthawizina ndimawazazira akazi wodula tsitsi lawo ndi kumavala zovala izi, ndipo nkumakhala ndi kumasungabe chodzinerera chawo cha Chikristu. Kumati, “Chimenecho ndi chinthu chaching’ono.” Chabwino, inu muyenera kuyambira penapake. Chotero muyambire pomwe apo, mu ma ABC anu. Mukuona? Ndipo muwadule mawonekedwe anu achidzikowo, mulimonse, ndipo mudzakhale wa mndende kwa Khristu. Ndipo mukatero muzingopitirira, kudula chirichonse chimasukepo, mpaka mzere wotsiriza utadulidwapo. Ndiye ndinu—ndinu. . . Inu ndi wa mndende pamene. Inu mumadzakhala mdzanja Lake. Iye, Iye amakugwirani inu mu dzanja Lake.

¹¹⁸ Tsopano, Mose ankadziwa kuti iye anali atabadwa ali wowombola. Iye ankadziwa zimenezo. Ndipo kodi inu munazindikira, ndi chokhumba chimene Mose anali nacho; akudziwa kuti amayi ake anali atamuza iye kumeneko, pakuti iwo anali womulera wake.

¹¹⁹ Sindikukaikira kuti, pamene Mose mwana wamng’ono yo anabadwa, kuti amayi ake anati, “Iwe ukudziwa, Mose, pamene. . . Adadi ako, Amramu, ndi ine timapemphera mosalekeza. Ife tinkadziwa, ndipo tinawona mu Mawu, inali itakwana nthawi yoti wowombola azibwera. Ndipo ife tinapemphera, ‘Ambuye Mulungu, ife tikufuna kuti tidzamuwone wowombola ameneyo.’ Usiku wina, Ambuye anatiuza ife, mu masomphenya, kuti iwe udzabadwa, ndipo iwe udzakhala wowombolayo. Ife sitinali kuwopa lamulo la mfumu. Ife sitimasamala kuti mfumu yanena chiyani. Komanso, ife timadziwa kuti iwe wabadwa uli wowombola. Tsopano, Mose, ife tinkadziwa kuti ife sitikanakwanitsa kukulera iwe moyenera.”

¹²⁰ Tsopano kumbukirani, iwo anali atakhala kumeneko, zaka foro handiredi ali mu Igupto. Mukuona?

¹²¹ “Ndipo ife—ife tinkafuna kuti tikupezere iwe—chinthu choyenera, maphunziro oyenera, kuphunzitsidwa koyenera. Chotero, ine ndinakutenga iwe ndipo ndinakakuika iwe mu kachombo kakang’ono, ndi kukakuyandamitsa iwe mu Nailo. Ndipo nzodabwitsa bwanji, kuti mafunde anatenga kachombo kakang’ono ako ndi kupita nako kudutsa mu mabango ndi mantcheza, ndipo anakakabweretsa iko uko, mamailosi kutali, ndi kukafikitsa iko mpaka ku nyumba yachifumu ya Farao, kumene wawo. . . mwana wamkazi wa Farao amakhala, kumene kunali malo ake osambira. Ndipo momwe kuti—kuti ine ndinadziwa kuti iye akanadzafuna mayi woti akakulele iwe.”

¹²² Ndipo mu masiku amenewo, zoono, iwo analibe mabotolo oti azimuyamwitsira mwana, kotero iye ankeyenera kuti akhale—namwino woyamwitsa. Chotero. . .

¹²³ “Ndipo, Miriamu, ine ndinamutumiza iye kumeneko. Ndipo iye anakaima kumeneko, ndipo iye anati, ‘Ine ndikudziwa kumene ine ndingakamupeze namwino woyamwitsa,’ ndipo anabwera ndi kudzanditenga ine. Ndipo, Mose, zitseko zonse zatsekeka. Wokonededwa, iwe uli usinkhu wa zaka sikisitini zakubadwa tsopano, ndipo iwe ndi woti ukhala mwana wamwamuna wa Farao. Ndipo tsiku lina iwe udzakhala wowombola amene ati adzawachotse anthu kuchokera kuno.”

¹²⁴ Zokhumba za Mose zinayamba kukula. “Ine ndiphunzira, amayi. Ine ndiphunzira chirichonse chimene ine ndingathe. Inu mukudziwa chimene ine nditi ndichite? Ine ndiphunzira momwe ine ndingakhalire munthu wa kunkhondo, ndipo ine ndidzadziwa momwe ndingawadzachotsere anthu awa kuno. Ine ndidzakhala general wamkulu, bishopu, mwakuti ine ndidziwa momwe zimachitikira. Ndipo ine ndika—ine ndikachita zimenezo. Ine ndikatenga Ph.D yanga kapena LL. Ine ndikachita zimenezo.”

¹²⁵ Monga “Bambo Chiniquy,” ngati inu munayamba mwawerengapo mabuku ake. Chabwino. Iyeyo “anali woti akawawombola Achiprotestanti onse,” inu mukudziwa, ndipo iye anadzakhala chimenecho, yekhayekha. Kotero, wansembe wamkulu uyu, zaka zapitazo, “Bambo Chiniquy,” inu muyenera kuti mukapeze bukhu lake ndipo mukaliwerenge ilo. Iwo amamutchula iye, “bambo.” Iye ndi M’bale Chiniquy basi, chimene izo zinali. Iye sitimamutcha munthu aliyense “bambo,” monga choncho. Kotero ife tikupeza kuti—kuti ife. . . Iye anali woti akawerenga Baibulo, kuti iye akapite uko ndi kukatsutsa chipembedzo cha Chiprotestanti ndi kukachipanga chonsecho kukhala Chikatolika. Ndipo pamene iye anapita kuti akawerenge Baibulo, Mzimu Woyera unabwera pa iye, ndipo iye analandira Mzimu Woyera, ndiyeno—ndiyeno iye anadzakhala mmodzi wa iwo.

126 Koteru ndiye zindikirani ichi, kuti Mose analandira kuphunzitsidwa konse. Chifukwa, i—iye ankadziwa. Iye anali wanzeru kwambiri, wophunzira kwambiri, waluntha kwambiri! Mpaka, palibepo aliyense... Iye ankakhoza ngakhale kuwaphunzitsa Achiigupto. Mpaka, iye ankakhoza kuwaphunzitsa owerenga maganizo awo. Iye ankakhoza kuwaphunzitsa ma—general awo chomwe mphamvu za ku nkondo zinali. Iye anali munthu wopambana. Ndipo anthu ankamuwopa Mose, chifukwa cha ukulu wake. O, kuphunzira koteroko! Mai! Iye anali bishopu wamkulu, kapena mwinamwake monga papa. Iye anali munthu wamkulu. Ndipo iye anali m—m—munthu wamphamvu. Ndipo iye ankadziwa kuti iye anabadwa kuti adzachite izi, ndipo anali ataphunzira, ali ndi kukhumba kwakukulu, kuti akachite zimenezo.

127 Chimodzimidzi monga lero. Ine sindikunena kuti amuna, amene akuphunzira mu masukulu awa, ine sindikunena kuti... Monga iwo ali kunja kuno Kumadzulo tsopano, iwo akukamanga sukulu ya madola mamilioni handiredi ndi fifite ya zaumulungu, mukuona, Chipentekoste, su—sukulu ya madola mamilioni handiredi ndi fifite. Kwa ine, amenewo ayenera kukhala mamishonare akukalalikira. Mukuona? Mukuona? Mukuona? Koma, chirichonsecho, kodi iwo amachita chiyani akatuluka kumeneko? Kodi iwo ndi chiani? Gulu la mashasha. Chimodzimidzi basi. Ndiyeno ndi momwe iwo amatulukirako. Izo nthawizonse zimatero, onse a iwo, ndipo ndi mzere womwewo. Mukuona?

128 Tsopano ife tikupeza kuti, kuti, pamene, Mose, mu kuphunzira kwake konseko. Ndipo lero, ndi kuphunzitsidwa konseku, kumapanga mabishopu aakulu ndi zina zotero, chikhumbo chachikulu, chapamwamba, kodi ife tichita chiyani? Zokhumba zathu zikumafika basi monga chimene Mose anali. Mukuona?

129 Mulungu, Iye asanamutenge munthuyo kuti akhale mdzanja Lake, Iye anachita kumuvula iye chikhumbo chake. Iye anamuvula iye kuphunzira kwake konseko.

130 Iye anapita uko, ndipo iye anakawombola; iye anakamupha wa chi Igupto mmodzi. Ndipo iye, ndipo pamene iye anatero, iye anakadzipeza kuti analakwitsa. Iye samayenera kuti achite zimenezo. Izo sizimayenera kukhala mwanjira imeneyo. Ndipo Mulungu anachita kumutengera iye ku tchile, ku chipululu, malo a chipululu.

131 Inu mukuzindikira, zokhala ngati zachilendo, momwe anyamata awa, amene Mulungu anali ndi uthenga wa kwa iwo. Iye amawatengera iwo ku chipululu.

132 Iye anamutengera Paulo ku chipululu, kuti akamuphunzitse, kuti akamuuze iye chimene masomphenya onse aakulu awa anali, anapita naye ku chipululu. “Anapita ku chipululu

chinachake.” Ndipo iye anakakhala kumeneko kufikira Mulungu atamudziwitsa kwathunthu choti akachite.

¹³³ Ndipo nthawi ya Mose, Iye anamutengera iye ku chipululu. Anakamusunga iye kumeneko kwa zaka forte, ndipo anamuvula iye zaumulungu zake zonse ndi chikhumbo chake. O, nthawi yakeyo, kuti iye amakhoza kuyang’ana mmbuyo ndi kuwona kulephera kwake. Ndipo momwe ife, usikuuno, tiyenera kuti tizichita chinthu chomwecho, pamene ife tiwona chokhumba chathu.

¹³⁴ Tayang’anani pa misonkhano ya machiritso, ndipo muwone ngati Mulungu anachita chinachake zaka pang’ono zapitazo, choti wayamba kubwezeretsa machiritso kwa odwala, ndi zina zotero.

¹³⁵ Aliyense, bungwe lirilonse, ndi chifukwa chakuti Izo sizinafike mu bungwe lawo, iwo anachita kukawatengera iwo mchiritsi. Ndipo kodi ife tachita chiyani? Tiyeni tiyang’ane pa izo mphindi chabe. Ife tachita chinthu chomwe chomwecho chimene Mose anachita. Ife tapita uko ndipo takayesera zolimba kuti tipukuse mtundu wina wa chozizwitsa. “Ine ndikununkhiza matenda. I—i—ine ndiri ndi magazi mdzanja langa,” ndi kupukusa chozizwitsa. Mukuona? Ndipo kodi ife tapeza chiani? Amuna ena chifukwa cha kupsyinjika kolimba uko, agawanika ndipo akakhala zidakhwa za nthawizonse, amanjenje, ndipo zagwira mmalingaliro awo. Ndipo iwo abwerera njira yonse mmbuyo, achoka ku dongosololo ku cholinga cha chipentekoste, abwerera kuti azikapanga mabungwe ndi zinthu kachiwiri. Mukuona?

¹³⁶ Kodi ife tachita chiyani? Tamupha pafupifupi mu Igupto mmodzi. Ndiko kulondola. Ndipo ife tayesera. Ife tazipanikiza. Ife talipira. Ife tavutikira, takhala utali wa usiku wonse mu misonkhano ya pemphero, mpaka ife kusasa mawu. Ndi—ndikuyesera kuti tipukuse chinachake, ndi kuthira msuzi chinachake, ndi mitundu yonse iyi ya zinthu, ndi kudzazipeza kuti zonsezo ndi zolephera kwathunthu. Ife tikusowa kuti tibwerere ku chipululu. Kulondola. Inde, bwana. Misonkhano ya misasa, ndi mavuto. Bwanji osangogonjera? Ndicho chimene inu muyenera kuti muchite, mukuona, mubwerere mmbuyo ndipo mukagonjere. Bwanji, ife tachita zinthu zomwezo zimene iwo anazichita, chinthu chomwecho chimene Mose anachita. Izo sizimachita ubwino uliwonse. Zitatha zaka forte, iye anadzazipeza yekha wa mndende ku Mawu a Mulungu. Kodi ife timayesera kuti tichite chiani?

¹³⁷ Pamene, Mdalitso wawukulu utulukira, ndi mawonetseredwe a zinthu zonse zazikulu izi zimene Mulungu watiuza ife: momwe ife tiyenera kuti tibadwe kachiwiri; momwe ife timalandirira Mzimu Woyera; ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu; ndi zinthu zonse izi apa.

138 Inu mukuona, anthu, mmalo moti azikhala ku Mawu amenewo, kukhala pa goli kwa Iwo, kodi iwo akuchita chiani? Iwo akuyamba ndi mbalume za chipembedzo chawo kumene, zimene zinali zitalephera kale, ndi kuyesera kuti apukuse chinachake kuti chiziwoneka ngati Choonadi.

139 Ine kuli bwino ndidulire pamenepo. Mukuona? Ine ndikutsimikiza ndinu a nzeru mokwanira kuti mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Mukuona? Koma, bwanji, taonani zimene izo zachita. Taganizani za zimenezo.

140 Kodi ife tiri ndi chiani, usikuuno, koma fu—fu—fuko longodzaza ndi anthu achibungwe amene akuwakana Malemba a Mulungu; amene akhoza kuwutcha m—m—Moyo wa Mzimu Woyera, kuti, “Iwo u—unali kuwerenga maganizo,” amene akhoza kukaniza zimenezo kuti zibwere mu tchalitchi chawo. Ndipo iwo sangakuloleze iwe kuti uwatchule Mawu amodzi a mbewu ya serpenti, chitetezero Chamuyaya, ndi zinthu zimene Mzimu Woyera waziulula ndi kuzitsimikizira kuti ndizo Mawu. Ine ndinawatsutsa ndi kuwatsutsa, kuti abwere ndi kudzazitsimikizira kwa ine kuti izo ndi zolakwika.

141 Kodi iwo ali ndi chiani? Chinthu chomwecho chimene Lutera anali nacho, onse a iwo, mukuona, anamupha wachi Igupto. Atani... Chinali chiani icho? Mwinamwake iye anamupanga munthu wina kuyamba... kusiya kuba, kapena mwinamwake kuti azikhala woona mtima kwa mkazi wake. Koma kodi inu munamupanga iye chiani kwa izo? Membala wa mpingo. “Bwerani ndipo mudzajowine gulu lathu.” Mukuona?

142 Munthu wakufa wonunkha uja chinali chinthu chokhacho chimene iye akanalozako zala zake, za kupambana kwake, za zaka forte za kuphunzira; wachi Igupto wonunkha atagona pamenepo, akuvunda ndiponso wakufa.

143 Umo ndi momwe ziliri usikuuno. Chinthu chokhacho chimene ife tingathe kuchiloza, kwa chitsitsimutso ichi chimene chawoloka (chotchedwa chomwecho), ndi gulu lonunkha la mamembala a mpingo amene sakudziwa zochuluka za Mulungu kuposa momwe Nkafula angadziwire za walupanga waku Igupto. Kulondola. Mpaka, ukawauza iwo za Mawu a Mulungu, iwo amati, “Ine sindimawakhulupirira Iwo.” Amati, “Ine sindikusamala zimene iwo akunena. Ine sindimawakhulupirira Iwo.” Mukuona? Mukuona? Ichho ndi chinthu choipa kwambiri kuti tizilozerako mmbuyo, pa zipsyinjo zonse ndi kuvutika ndi chirichonse zomwe ife tiri nazo.

144 Mwinamwake ife tikhoza kulozera kwa sukulu yaikulu, koma iyo ndi yakufa. Ife tikhoza kulozera kwa bungwe, koma ilo ndi lakufa. Ilo likununkha. Ziri ngati chinthu choyamba chimene ife tinachokako. “Monga nkhumba kubwerera ku matope ake, ndi galu ku masanzi ake,” pamene ife tibwerera mmbuyo. Wachi Igupto mmodzi wakufa.

145 Nzosakaikitsa koma wina anati, “Mose, chabwino, kodi ulibenso kukhudzidwa ndi anthuwa? Iwe unaitanidwira ichi.” Winawake amene ankamudziwa Mose, ankadziwa kuti iye anaitanidwira chimenecho. “Ndipo osati...Iwe ulibe kukhudzidwa ndi anthuwa?”

“Ayi, bwana.”

146 “Chabwino, bwanji iwe sukupita, uko, kumakachita *izi*? Ndipo bwanji iwe sukubwera kuno, kudzayesa *izi*? Ndipo nanga bwanji iwe sukupitirira ndi onse a iwo?”

147 Mose anali ali kunja uko akuvulidwa, kufikira kuti iye anakhala ndi chomuchitikira pa chitsamba chonyeka, chimene chinanena Mawu akuti. “INE NDINE Mulungu wa Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo. Ndipo Ine ndikukumbukira malonjezo Anga. Ndipo Ine ndabwera kuti ndidzawawombole iwo. Ine ndikukutuma iwe kuti ukachite zimenezo.” Izo zinali zimenezo.

148 Iye anawawona Mawu, osati chokhumba cha anthuwo kapena zokhumba za anthu. Ndiye kodi iye anadzakhala chiani? Iye sanafune kuti aziwawonanso Aigupto apanso. Iye sanafunenso kuti azikumanizana nacho chinthu ichi apanso. Koma iye anadzakhala wa mndende. Amen. Zaka forte zakuthawa, akumuvula, komano iye anadzakhala wa mndende, pa chitsamba chonyeka, Mose wamphamvu ali ndi luntha lonse. Baibulo limanena kuti Mose anali munthu wamphamvu mu mawu kapena mu ntchito, uko mu Igupto.

149 Koma taonani zimene wazaumulungu wamphamvuyo anachita Pamaso pa chitsamba chonyeka. Iye anangovemereza kusatha kwake. Pamene iye anachiwona cholinga chenicheni cha Mulungu, iye anavomereza kuti iye anali wosatha kuti akachite izo. Komabe, iye anaphunzitsidwa mu zaumulungu zonse zimene iwo akanatha kumupatsa iye, anaphunzitsidwa mu sukulu yawo yapamwamba. Koma, apobe, iye akanakhoza kuchita chiyani pamene iye...Lawi la Moto lija litapachikika apo pa chitsamba? Anati, “Ine sinditha nkomwe kulankhula naye Iye. Ambuye, ndine ndani, kuti ndipiteko?” Mukuona?

150 “Vula nsapato zako, Mose. Ine ndikufuna kuti ndilankhule ndi iwe. Udzivule wekha mpaka pansu, ngakhale nsapato zako. Iwe—iwe wabwereranso pansu kachiwiri. Ine ndikufuna kuti ndilankhule ndi iwe.”

151 Samatha ngakhale kuti alankhule. Potsiriza, wa mndende wosankhidwa, mneneri wosankhidwa, chimodzimidzi monga Paulo uja anasankhidwa. Mose anasankhidwa, wowombola. Ndiyeno, potsiriza, Mulungu anali naye munthu Wake wosankhidwa wa mndende kwa Iye. O, aleluya! Iye amakhoza kokha kuyenda pamene Mawu a Mulungu amuyendetsa iye. “Ndikati wandituma ine ndi ndani?”

“INE NDINE.”

“Kodi ine ndikachita motani?”

“Ine ndikakhala ndi iwe.”

152 “Inde, Ambuye, monga Inu mwanenera. Ndine pano.” O, mai! Kuti, iye ndi wa mndende.

153 Iye akupita motsutsana ndi kaganizidwe kake kabwino. Tsopano, iye anali ataphunzitsidwa kuti azilamulira ankhondo. “Malupanga, mmwamba! Kutembenukira kumanja!” Anaphunzitsidwa kuti azipita, “Magareta, onse ali mu dongosolo! Mivi, patsogolo! Menyani!” Umo ndi momwe ati akalitengere ilo. Umo ndi momwe anaphunzitsidwira.

Koma iye anati, “Kodi ine ndikagwiritsa ntchito chiyani?”

Anati, “Uli ndi chiyani mdzanja lako?”

154 “Ndodo.” Mulungu amachita zinthu monyozeka kwambiri nthawizina, kwa malingaliro a munthu. Mukuona? Anali ndi ndodo mdzanja lake. Ndevu zikuzendewera pansi. Usinkhu wa zaka eyite. Mkazi wake ali pa bulu; mwana atakhala pa ntchafu yake. Mikono, yaing’ono yakale yofooka ikuzendewera pansi; ndodo. Atangodzutsa mutu wake, pakuti iye anali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Bwanji? Iye potsiriza anali atazikika.

155 Iye anali wa mndende. “Ine ndizingosuntha pamene Mawu akundisuntha ine. Ine ndizingolankhula pamene Mawu akulankhula.”

“Kodi ukupita kuti?”

156 “Ine ndiri ndi kutuma kumodzi: kukaima pamaso pa Farao ndi kukamusonyeza iye, ndi ndodo iyi, kuti Mulungu wandituma ine.” Ameni.

“Ukachita chiyani zikakatha zimenezo?”

“Iye akapereka chinthu chotsatiracho, ine ndikakatha kuchita ichi.”

157 Ndi zimenezotu. Inu mwangotsala ndi chinthu chimodzi chokha kuti muchite, sitepe yoyamba, usikuuno: mugonjere, mukhale wa mndende. Musadziganizire za inueni kapena china chakenso. Mukhale wa mndende.

158 Mose anadzakhala wa mndende, anavomereza kuti iye samatha nkulankhula komwe. Potsiriza, pamene Mulungu anadzamugwira iye mdzanja Lake, pamene iye amangoyenda pamene Mulungu amuyendetsa iye. Pamene, Iye anamuuza iye Mawu. Iye ankadziwa kuti iwo anali Mawu, ndiye iye anadzipereka yekha ku Mawu. Ndipo Mzimu Woyera pamenepo, Mulungu, anamumanga goli Mose ku chifuniro cha Mulungu.

159 Ndicho chinthu chomwecho chimene Iye anachita kwa Paulo. Kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye anamumanga goli Paulo; Myuda wamng’ono, wa mphuno ya ngowe, wachipongwe, o, wokhala ndi Ph.D. ndi LL.D zitalembedwa paliponse pa iye. Koma Iye anati, “Ine

ndimusonyeza iye zomwe iye ati azimve kuwawa chifukwa cha Mawu.” Mukuona? Ndipo iye. . .

¹⁶⁰ Ndiyeno Paulo atakhala pamenepo ndipo akuwawona Mawu, ndi kumawona kuti ameneyo anali Yesu, ndiye iye anakweza manja ake mmwamba ndipo anadzakhala wa goli kwa Iye. Chikondi cha Mulungu chinamumanga iye goli kwa Mawu. “Iye akatengera Dzina Langa pamaso pa Amitundu.” Kumeneko iye anapita.

¹⁶¹ “Mose, INE NDINE Mulungu wa makolo ako. INE NDINE Mulungu wa Abrahamu, Isaki, ndi wa Yakobo. Ine ndikukumbukira Ine ndinawalonjeza iwo, ndipo nthawi ya lonjezolo yayandikira. Ndipo Ine ndawona mazunzo a anthu Anga. Ine ndakumbukira lonjezo Langa. Ndipo Ine ndabwera kuti ndidzakumange iwe goli. Inu mukudziwa chimene Mawu ananena. Ine ndakumanga iwe goli kuti upite kumeneko, ndakumanga goli ndi mphamvu, kuti upite kumeneko ndi kukawawombola anthu Anga. Ndipo utenge ndodo imeneyo ili mdzanja lako, ngati umboni, chifukwa iwe wawona chozizwitsa chikuchitidwa ndi iyo.” Basi monga Davide, ali ndi legeni. Mukuona?

¹⁶² Anadzimanga goli, yekha, ndipo iye anapita kumeneko. Potsiriza, Mulungu anali ndi munthu amene anali womumvera Iye, anamangidwa goli kwa Iye, ndipo iye samatha kusuntha kufikira Mawu a Mulungu atamusuntha Iye. Ngati anthu atangochita zimenezo, lero! Ndiye, iye anali wamndende Wake, wa mndende wa chikondi, anamangidwa goli mu nsinga za chikondi, ndi—ndi Mulungu, monga Paulo anamangidwa goli mu nsinga za chikondi cha Mulungu.

¹⁶³ Chimodzimodzi monga Paulo, awiri onsewo anaphunzitsidwa mwanjira yofanana. Mose anaphunzitsidwa, inu mukudziwa, kuti akawawombole ana a Israeli ndi mphamvu zaku nkondo. Paulo anaphunzitsidwa kuti akawatulutse iwo kuchokera mmanja a Achiroma ndi kukawamasula iwo, ndi mphamvu yake yaikulu yachipembedzo mu dziko tsiku limenelo. Masukulu apamwamba a kuphunzitsa, ankakhala panso pa Gamalieli.

¹⁶⁴ Ndipo awiri onsewo anapita ku chipululu; anabwererako ali amuna osinthika. Awiri onsewo anawona Lawi la Moto. Ndipo awiri onsewo anali aneneri. Kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Awiri onsewo, aneneri. Ndipo iwo onse analankhulidwa ndi Lawi la Moto, kulondola ndendende, kubwerera wowombola. Ndi awo apo; anapita ku chipululu. Anasiya nyumba zawo ndipo anapita ku chipululu, kuti akafufuze. Anawasiya anthu awo ndi chirichonse, kuti akafufuze chifuniro cha Mulungu. Mukuona?

¹⁶⁵ Iwo anaphunzitsidwa mwanjira ina; Mulungu anawasinthira iwo ku ina. Ndipo iwo ankayenera kuti adzakhale amndende

kwathunthu, kuti asamakachitenso mwanjira yomwe ankafuna kuti azikachitira, koma kumakachita mwanjira imene Mulungu ankafuna kuti iwo azikachitira. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

¹⁶⁶ Kodi ife tiri nawo maminiti teni ena pamenepo, kuti ndikwanitse izi? [M'bale Neville akuti, "Ameni."—Mkonzi.]

¹⁶⁷ Ine mwamsangamsanga ndifika kwa munthu wina. Ine ndikumuwona wina patsogolo panga tsopano. Dzina lake Yosefe. Iye anali mwana wosankhidwa. Iye anali choimira changwirowo cha Yesu Khristu. Iye anabadwa ali mneneri. Iye anali mneneri, nayenso. Mukuona? Ndipo tsopano iye amakhoza kuwona masomphenya. Ndipo pamene iye anali akadali mwana wamng'ono, iye anawona masomphenya a iyemwini atakhala pa mpando wachifumu, ndipo azibale ake akumulambira iye. Mukuona? Koma penyani. Iye anadzakhala...Iye anadzimva ngati kuti iye anali munthu wapamwamba. Mukuona? Onse a iwo...

¹⁶⁸ Koma kodi Mulungu anachita chiani? Iye anachita chinthu chomwecho chimene Iye anachita kwa onse a iwo. Chifukwa, Mose anali wowombola, Paulo anali wowombola, ndipo tsopano Yosefe anali wowombola. Iye anawapulumutsa anthu ake ku njala.

¹⁶⁹ Kodi Mulungu anachita chiyani kwa iye? Anakamuika iye mu ndende, anakamuika iye molunjika ku ndende. Inde, bwana. Kumbukirani, iye anagulitsidwa ndi abale ake, kwa wa chiIgupto. Ndipo iwo anakamugulitsa iye kwa Potifara. Ndipo Potifara anamupatsa iye ufulu pang'ono, ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, zimenezo zinadzachotsedwa kwa iye. Ndipo apo iye anakakhala mu ndende, akulira, akulira. Mulungu amayenera kuti amuvule izo.

¹⁷⁰ Tsopano zindikirani. Koma, nthawi yonseyo, ine ndikukhulupirira, iye, mu ndende imeneyo, iye amakhoza kukumbukira kuti masomphenya ananena kuti iye akanadzakhala pa mpando wachifumu, ndipo abale ake anali woti azikumulambira iye, chifukwa iye ankadziwa kuti mpatso yake ndi yochokera kwa Mulungu. Ndipo iye ankadziwa kuti izo zimayenera kuti zidzakwaniritsidwe.

¹⁷¹ Ngati ife titati tazinga izo mmalingaliro athu, ndiponso mogwirizana ndi Mawu a Mulungu, kuti mu masiku omaliza ano Iye akhala nawo Mpingo, Iye akhala ndi anthu. Ndipo zinthu izi zimene Iye analonjeza, Iye azichita izo. Iye anati Iye akanadzazichita, ndipo ife tikukhala mu nthawi imeneyo. Ife tiri kumeneko. Iye akungoyesera kuti atitenge ife tikakhale a mndende enieni tsopano, otsekeredwa mkati limodzi ndi Iye.

¹⁷² Inu munaimva nyimbo yakale ija yomwe inu mumaiyimba, "Ndiyeno ine ndatsekeredwa mkati ndi Mulungu"? Ine ndikufuna kuti nditsekeredwe mkati ndi Mulungu. Tsopano,

ndi pamene ine ndinaganizira za izi. Kukhala utatsekeredwa mkati ndi Mulungu, osati chinanso, ndipo iwe nkumangosuntha pamene Mulungu akuti usunthe. Iwe nkumangochita pamene Mulungu akuti uchite, mwaona, ndiye kuti ndiwe wotsekeredwa mkati limodzi ndi Mulungu.

¹⁷³ Tsopano kumbukirani, iye anali kuganiza. Iye nayenso anadzakhala wolephera kwathunthu, kwa iyemwini. Zonse zomwe iye ankazidziwa, zonse zomwe iye ankazimvetsa, ndi chirichonse, iye anadzakhala wolephera kwathunthu. Izo sizinagwire ntchito. Iye anadzaikidwa pansi pa chochitika chakuti panalibe aliyense akanamumvera iye. Iye anali wa mndende. Mukuona? Iye anaikidwa mu chikhalidwe, chimene osakhulupirira sakanamukhulupirira. Kodi inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Utumiki wake unali wopanda mphamvu. Anthu anapotoloza mitu yawo. Iwo samakhala ndi chidwi kwa iye mu ndende. Kodi ndi chabwino chanji chimene utumiki wake ukanachita? Iye mwina amakhoza kuima pa zitsulo za mndende ndi kumalalikirira kwa iwo; iwo amakhoza kumayenda akutsika msewuwo. Mukuona? Koma iye anadzakhala wa mndende. Ndipo Mulungu anamusunga iye, wa mndende, kufikira gudumulo litagudubuzika molondola. Anati, “Ndi ameneyu munthu Wanga.” Ulemerero! Wolephera kwathunthu!

¹⁷⁴ Potsiriza, Mulungu anabwera kwa iye mu ndende. Monga Paulo, monga ena onse a iwo, iye anabwera kwa iye. Ndipo Iye anagwiritsa ntchito mphatso imene Iye anamupatsa iye, kuti ikamutulutse iye mmenemo. Ndiko kulondola. Iye anamuchotsako iye ku ndende yake. Kodi iye anachita chiyani? Mwamsanga pamene Iye anamuchotsa iye ku ndende, iye anapatsidwa mphamvu ndi mfumu, mfumu yake, yomwe iye ankakhala pambali pake, yemwe anali pansi pake. Iye anabweretsedwa kuchokera ku nyumba ya ndende ndipo anapatsidwa mphamvu; mpaka, chirichonse chimene iye amanena, chimayenera kuchitika. Amen.

¹⁷⁵ Mu ndende yake, mosalekeza iye ankakumbukira, iye anabadwa kwa cholinga. Iye anali woti adzakhala pafupi ndi mfumu. Ena onse a iwo anali oti adzagwaditsa bondu kwa iye. Masomphenya ake ankamuza iye chomwecho. Amen. Koma masomphenya akewo asanakwaniritsidwe kwathunthu, iye anali atakhala wa mndende. Amen. Ndipo kenako iye anadzakhala wolamulira. Ndipo pamene iye anabwera kuchokera ku nyumba ya mndende, ndi kudzakhala wa mndende wa Mawu a Mulungu, kuti iye amakhoza kulankhula kokha zimene Mulungu waika mkamwa mwake kuti azinene, pamenepo Mulungu amayenda kudzera mwa iye.

¹⁷⁶ Zindikirani, kuti Mose anali nazo mphamvu zokhoza kuwamanga akalonga a Farao, pomwe iye angafunire. “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Suntha.’” Iye anali nazo

mphamvu zokhoza kuwamanga akalonga a Farao. Kaya iwo anali madikoni, kapena oyang'anira, kapena iwowo ndi oyimira a boma kapena chirichonse chimene iwo anali. Iye akati, "Ine ndikukumangani inu," ndipo iwo amakhala atamangidwa. Zinali zimenezo izo. Iye amakhoza kuchita zimenezo mwa mawu ake omwe, momwe iye zingamusangalatsire. Amen. Ulemerero kwa Mulungu!

O, ine ndangotsala ndi maminiti atatu owonjezera, kotero ine ndisunge mawu anga.

¹⁷⁷ Tsopano ife tikupeza, kuti iye—iye anadzakhala wa mndende kwa Mulungu, kuchokera kwa wa mndende wa mdziko. Kuchokera . . . Paulo, chimodzimidzino. Ndipo Mose, mwanjira yomweyo, kuchokera kwa wa mndende wa maganizo ake ake, kukakhala wa mndende wa Mulungu. Ndipo pamene iye anatuluka, iye anali ndi mphamvu ya Mulungu. Ndipo pamene iye anadzakhala Paulo . . . Pamene kuganiza kwakale, kwa Mose, iye anadzipereka izo ndipo anavulidwa izo, iye anadzakhala wa mndende kwa Mawu a Khristu. Amakhoza kokha kusuntha pamene . . .

"Inu mukuti, 'Khristu?'"

¹⁷⁸ "Iye anachiyesa chitonzo cha Khristu chuma chochuluka kuposa icho cha Igupto." Kotero iye anali wa mndende kwa Khristu, chimodzimidzi monga Paulo analiri.

¹⁷⁹ Kumbukirani, atatu onse a iwo anali aneneri. Mukuona? Ndipo iwo ankayenera kuti avulidwe kuganiza kwawoko, ndi cholinga chakuti adzakhale a mndende kwa chifuniro ndi njira za Mulungu.

¹⁸⁰ Ndiye ife tikukumbukira, tsopano, kuti iye anali ndi mphamvu zokhoza kumanga, iyeyo akalankhula. Iye anali ndi mphamvu zomasula, iyeyo akalankhula. Iye amakhoza kunena kuti, "Ine ndakumasula iwe, mu dzina la mfumu yanga." Amen. Farao anamupanga Yosefe kukhala mwana wake.

¹⁸¹ Khristu akuwapanga, a mndende Ake achikondi, kukhala ana Ake. Ndipo Iye akuwapatsa iwo mphamvu, chinthu chomwecho chimene Iye anali nacho. Yohane Woyera 14:12, "Iye amene akhulupirira pa Ine, onani, ntchito zimene Ine ndikuzichita nayenso azidzazichita. Ngakhale zochuluka kuposa izi azidzazichita." Tsopano wa mndende wa chikondi cha Khristu akudzapatsidwa mphamvu ndi Mfumu yake, Yemwe ali Khristu. Amen. "Ndipo indetu Ine ndinena ndi inu, ngati inu mudzanena kwa phiri ili, 'Suntha,' ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti zimene inu mwazinena zidzazichitika, inu mudzalandira zimene inu mwazinenazo. Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga akakhala mwa inu; ngati inu muli pa goli kwa Ine," chifukwa Iye ndi Mawu Ake ali zofanana. "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu. Mawu anadzasandulika thupi ndipo anadzakhala

pakati pathu. Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Ngati inu mukhala mwa Ine,” osati umu *apa* ndi *apo*. “Mukakhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga mwa inu; mupemphe chimene inu mukufuna, kapena munene chimene inu mukufuna, icho chidzachtidwa kwa inu.” Iye anali nazo mphamvu.

¹⁸² Zindikirani, iye asanatuluke, iye ankayenera kuti atulutsidwe ndi kumetedwa. Zinthu pang’ono zimayenera kuti zimetedwe iye asanati akakomane ndi mfumu yake. Mukuona?

¹⁸³ O, Mulungu nthawizina amawatengera anthu Ake kunja monga choncho, ndipo amakawameta zofuna zawo zapang’ono, kukawasonyeza iwo kuti iwo sangathe basi kuchita zimene iwo akufuna kuti achite. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Iwo siali—iwo samakhala pa ufulu kuti azichita zimene iwo akufuna kuti achite. Iwo asanafike pokhala ndi mphamvu yathunthu ndi kudzakhala kapolo wa chikondi kwa Khristu, iwo amayenera kuti ametedwe ndipo kenako aperekedwe. Nthawizina Iye amawatengera iwo ku chipululu, kuti akachite zimenezo, kuti akawamete iwo. Ndipo akatero amawatulutsako iwo, iye wodzozedwayo, kuti akakwaniritse cholinga chimene Iye anawadzozera kuti iwo adzakhale. Mukuwona chimene ine ndikutanthauza?

Abale, ife tiri pamapeto a nthawi.

¹⁸⁴ Kumbukirani, nthawi zina zonse, zimene Iye amachita. Iye nthawizonse amayenera kuti amutenge munthu ndi kudzamupanga iye wa mndende kwa Iye, amazisiya zake zomwe. Iye amachita kuzisiya zonse zomwe iye ankazidziwa, amaiwala zophunzitsidwa zake zonse, chirichonse, ndi cholinga chakuti akadziwe chifuniro cha Mulungu, ndi kukamutsatira Mulungu.

¹⁸⁵ Iye samatha kutsatira chirichonse chimene munthu akuchita, ndi Mulungu, nthawi yomweyo. Ndi zotsutsana, china kwa chimzake. Iwe sungamapite kummawa ndi kumadzulo pa nthawi yomweyo. Iwe sungamapite kumanja ndi kumanzere pa nthawi yomweyo. Iwe sungamachite chabwino ndi choipa pa nthawi imodzi. Iwe sungamamutsatire munthu ndi Mulungu pa nthawi imodzi. Ayi, bwana. Iwe mwina ukutsatira Mulungu kapena ukutsatira munthu.

¹⁸⁶ Tsopano, ndiye, ngati iwe ukutsatira Mulungu ndipo wadzipereka wekha kwa Mulungu, ndiye iwe umadzakhala wa mndende kwa Mulungu ameneyo, kwa Mawu amenewo, kwa chifuniro chimenecho. Ziribe kanthu zimene china chirichonse chikunena, iwe umadzakhala wa—wa mndende kwa Iwo.

¹⁸⁷ Mvetserani. Ife tiri pamapeto a nthawi. Ndipo ine ndinganene izi ndi ulemu ndi kulemekeza, pamene maminiti otsiriza angapo akudutsa. Taonani. Chimene Mulungu, mwakuganiza kwanga, ati adzachite ndipo ayenera kuchita, ndipo adzachita mu tsiku lomaliza ili, ndi kuti apeze chida chokololera. Iye ayenera kuti apeze chida, kuti akapunthire

padwale. Mlimi aliyense, pamene iye akupita kuti akakolole, iye amayenera kuti akhale ndi chida choti akachitire zimenezo; ndithudi, iye amayenera kukhala ndi chikwakwa chakuthwa kapena chinachake, chida chinachake, kuti akamwetere mbewuzo. Ndipo zokolola zacha.

¹⁸⁸ Mulungu, mutitengere ife mdzanja Lanu. Mutipange ife antchito-ammusinga ya chikondi Chanu. Mutigwiritse ife ntchito ngati chida, kuti tikabweretse kuzindikira kwa dziko lapansi lochimwa, lotembereredwa ili limene ife tiri kukhalamo lero, kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

¹⁸⁹ Kwa inemwini, Mulungu, mudirole ine ndikhale wa mndende. Ngati abale anga onse andikana ine, ngati azimzanga onse andikana ine, ine ndikufuna kuti ndikhale wa mndende wa Yesu Khristu ndi Mawu Ake, kuti ine ndikakhoze kukhala wa goli kwa Mawu Ake, mwa Mzimu Woyera, kuti ndikawuwone Mzimu Woyera ukuwapanga Mawu a Mulungu kumaatsimikiziridwa mwa zinthu zomwezo zimene Iye anati zikanadzachitidwa. Ine ndikufuna kuti ndikhale wa mndende wa Yesu Khristu.

Tiyeni tipemphere.

¹⁹⁰ Ine ndikudabwa, usikuuno, ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ngati chikhumbo chija chimene ife tiri nacho, cha kukhala chinachake, kapena mwinamwake cha chinachake chimene ife tingathe kuchiganizira, kaya ndi chinthu chodzikhonda, ndikudabwa ngati ife sitingathe kungokhala ngati tachiyika icho pambali.

¹⁹¹ Ine ndikudabwa ngati mnyamata wina pano, usikuuno, akuyang'anayang'ana, ndikuti, "Ine ndidzakhala, pamene ine nditi ndidzakule, ine ndidzakhala chinthu *chakuti-chakuti*." Ndikudabwa ngati iwe ukukhoza kumverera chifuniro cha Mulungu chikuyenda mmoyo wako, ndi kuti, "Ayi, ayi. U-huh. I—ine . . . Zokhumba zanga zatayika tsopano. Masiku pang'ono apitawa, Mzimu Woyera wakhala ukulankhula ndi ine. I—ine—ine—ine ndikufuna kuti ndidzipereke ndekha kwa Mulungu, kuti ndikakhale chida chopunthira cha tsiku lomaliza lino."

¹⁹² Mtsikana wina wamng'ono amene angakhale ndi zikhumbo za dona wa khalidwe labwino, ka—kapena mwinamwake kangenge kokongola kakang'ono, kapena mwinamwake tsiku lina kudzapanga Hollywood ngati ntchito yanu, i—ine ndikudabwa ngati inu simukulolera tsopano kuti mupereke chokhumba chanu Pamaso pa Mulungu ndi Mawu Ake, kumva kuitana kwa Mulungu mu moyo wanu womwe. Mulungu akudziwa yemwe inu muli.

¹⁹³ Ine ndikudabwa ngati pangakhale mtumiki pafupi, kapena wantchito, wantchito kwina wake mu tchalitchi. Ine ndimangobwera muno, apo ndi apo. I—ine sindikudziwa theka

limodzi la atatu la anthu amene akhala pano, usikuuno, koma ine . . . apang'ono okwanira mdzanja awa pano. Ine ndikudabwa ngati pangakhale munthu woteroyo, amene mungakhale wololera kunena kuti, "Ine sindikusamala zimene aliyense akunena. Ndine kapolo wa Mulungu tsopano. I—ine—ine ndikukalalikira Mawu Ake, mulimonse. Ine sindikusamala kuti, bungwe langa—langa lindikana ine, ine ndikhala nawobe Mawu amenewo. I—ine ndikachita zimenezo. Chifuniro changa ndi chifuniro cha Mulungu. Chifuniro cha Mulungu ndi chifuniro changa. Ine ndikupita kukakhala wa mndende kwa Yesu Khristu. Mwa chisomo Chake ndi thandizo, ine ndikachita zimenezo."

¹⁹⁴ Taganizani za zimenezo, pamene ife taweramitsa mitu yathu. Ndi angati ali ndi chikhumbo chimenecho, usikuuno? Kodi mungakweze dzanja lanu. Ndi changanso, inenso. Ine ndikupereka zonse. Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano, mwachifatse tsopano, pamene inu mukulingalira zimenezo tsopano, pamene inu mukupemphera.

Ndipereka zonse,
Ndipereka zonse,
Zonse kwa Inu, Mpulumutsi wanga wodala,
Ndipereka zonse.

Ndiperek- . . .

¹⁹⁵ Kodi inu mukutanthauza kwenikweni zimenezo? "Ine ndikufuna kuti ndikhale wa mndende. Ine . . . Munditenge ine, Ambuye. Munditengere ine ku nyumba ya Wowumba, usikuuno. Mukangondiswako ine yense, ndipo mukandiwumbenso ine kachiwiri, mpaka pansu."

Kwa inu, Mpulumutsi wanga wodala,
Ndikupereka zonse.

¹⁹⁶ Atate Akumwamba, pamene nyimboyo ikupitirira kumaimba, ine ndinaganiza kuti ndi chaphindu kwambiri pa nthawi ino, kuti i—ine ndidukizire pa nyimboyo ndi kulankhula ndi Inu mphindi chabe. Pamene anthu akulingalira, "Ine ndipereka zonse," Atate, mulole ife tikachite ichi, ngati kuti uwu ndi mwayi wathu womaliza woti tichitire izi. Mutilole ife tibwere ndi kuwona mtima, tibwere pa gome la Ambuye, moga momwe zinaliri, ndi zovala zochapidwa, miyoyo yochapidwa, zifuniro zochapidwa, zokhumba zochapidwa, kuti tikadzipereke tokha.

¹⁹⁷ Ndi kumulola Mulungu kuti atenge Mawu Ake, kutimanga goli ife limodzi ndi Iwo, Mawu a Mulungu. Ndipo mulole Mzimu Woyera utitenge ife tsopano, pamene ife tikumva kulira kwa joko pozungulira mitima yathu, "Kuyambira usikuuno, Ine ndizikutangani inu pa mawu anu. Tsopano musamaganize mwa kuganiza kwanu kwanu. Muziganiza malingaliro Anga. Muziganiza chifuniro Changa. Ine ndizikutsogolerani inu."

Mulungu, mupereke kuti chikakhale chotichitikira kwa mmodzi aliyense wa ife.

¹⁹⁸ Anyamata awa amene akhala pano; mwamuna ndi mkazake; ndipo ena abwera kuti adzakhale mwamuna ndi mkazake. Pali anthu achikulire akhala pano, amene ali atumiki, akhala ali pa msewuwu. Ndipo, Ambuye, pano pali M'bale Neville, ine, ife tikukwera pamwamba pa makwerero. Masiku athu akuhepera chepera tsopano. Masitepe athu akupangidwa kukhala osamalitsa kwambiri kuposa momwe ife tinkawapangira iwo. Ife tikumasamalitsa pamene ife tikupondapo. Ife sitiri ojaira-maponedawe, kulankhula mwa chithupi, monga ife tinkachitira nthawiyina. Koma, Ambuye, pamene ife tikuwona moyo wachivundi uwo ukuzilala, ndipo palibe a masitepe athu amene amakhala ojaira popanda Inu kutigwira dzanja.

¹⁹⁹ Tsopano, Mulungu, mutitenge ife, kodi mutero Inu? Mutenge mitima yathu ndi kufuna kwathu zikhale mdzanja Lanu Lomwe, ndipo mutilole ife tikakhale a mndende, usikuuno, kwa Mawu, kwa Khristu. Mulole ife tikakhale miyoyo yaumulungu kuno. Mulole akazi awa, atsikana awa, anyamata achichepere awa, anyamata ndi atsikana, apereke moyo wawo, Ambuye. Ndipo mulole chokhumba chawo chidzakhale chokhumba chakuti azikamutumikira Yesu Khristu. Ndipo mutilole ife tisanduke a mndende a chisomo Chake Chaumulungu ndi chifuniro. Perekani izi, Ambuye.

²⁰⁰ Ndizo zonse zimene ine ndimadziwa kuzichita, Ambuye. Mawu osweka-sweka apang'ono awa, ndipo i—ine ndikudalira kuti Inu muwayika iwo pamodzi, molondola. Chifukwa, mukutantha muno, ndipo anthu akufuna kuti amvetsere, koma mwatantha kwenikweni. Ndipo ambiri ayenera kuti azipita kwawo ndipo akapite ku ntchito molawirira. Koma mulole mbewu zimenezo zikangowera mu mtima wawo, “wa mndende.”

²⁰¹ Apite kunyumba ndipo akanene kwa mkazi wawo, pamene iwo...iwo asanakonzeke kuti agwade ndi kupemphera, madzulo ano, kapena usiku uno, pambali pa bedi, akayang'anizane wina kwa mzake, ndikuti, “Wokonedwa, nanga bwanji zimenezo, usikuuno? Kodi ife takhaladi amndende kwa Khristu ndi chifuniro Chake, ka—kapena kodi ife tikugwirira ntchito chifuniro chathu chomwe?”

²⁰² Mulole anyamata ndi atsikana, paliponsepo, makamaka iwo amene amva Uthenga, usikuuno, adzifunse okha funso lomwe lomwelo, “Kodi ndine wololera kuti ndikhale wa mndende, kuwusiya moyo wanga womwe?”

²⁰³ “Iye amene awupulumutsa moyo wake adzawutaya iwo, koma iye amene ati adzawutaye moyo Wake chifukwa cha Ine adzawupeza iwo.” Atate, ife tikudziwa, kuti izo ndi: kukhala wa mndende wa Inu, kutaya zokhumba zathu zomwe ndi zofuna

zathu zomwe, kuti tikapeze Zanu, tikatero ife tidzakhala nawo Moyo Wamuyaya. Perekani izi, Ambuye.

²⁰⁴ Chinthu chokhacho chimene ine ndikuchidziwa, ndi kuzipereka izo tsopano mdzanja Lanu. Ndipo mulole izo zikakhale zobereka zipatso ndi kubweretsa zida zazikulu—zazikulu zokololera kwa tsiku lomaliza, amuna ndi akazi, anyamata ndi atsikana, kudzipereka kwa chifuniro chathunthu cha Mulungu, ndi kudzakhala amndende a Yesu Khristu, kwa chikondi Chake, omangidwa ndi zingwe za chikondi Chaumulungu kwa Khristu. Ife tikupempha izi mu Dzina Lake.

Ndipereka zonse,

Tiyeni tiimirire.

Ndipereka zonse,

Zonse kwa Inu, wanga . . . ? . . .

²⁰⁵ Tiyeni tingonena zimenezo apanso, ndi maso athu otsekedwa ndi manja athu mmwamba.

Ndipereka zonse,

Ndipereka zonse,

Zonse kwa Inu, Mpulumutsi wodala,

Ndipereka zonse.

²⁰⁶ Tsopano, ngati ife tingaweremitse mitu yathu, ndipo nyimbo yobalalikira isanaimbidwe, ya *Tenga Dzina La Yesu Ndi Iwe*. Ine ndifunsa kuti—kuti m'bale uyu apa . . . ine ndaiwala dzina lake. Mlongo amene anachitira umboni za masomphenya a mdima ukubwerapo, amene anachiritsidwa. Ndipo kumbukirani, atayang'ana mmbuyo, chophimbacho chinali chitapita. Chikhulupiriro chake chinachita zimenezo. Inu mutibalalitse ife mu pemphero, kodi mutero inu, m'bale? Ndi kupempha madalitso a Mulungu pa ife.



WAMNDEDE CHA63-0717
(A Prisoner)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu usiku, Julaye 17, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2015 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org